

**KOTALE WA  
ACHINYAMATA**

**JULY- DECEMBER,  
2023**

## **MAWU OYAMBA**

Gawo lino la kotale wathu tionamo zambiri zokhunza moyo wathu wa tsiku ndi tsiku ife achinyamata ndi moyo wa uzimu. Mu maphunziro athu ena m'mbuyomo tidaonanso za achinyamata ndi moyo wa makono, tidaonanso nkhani yokhunza chikhulupiriro chathu kuti achinyamata ambiri tidathandizika kudziwa chomwe ife tili. Tsono tikupempheni kuti wachinyamata aliyense akhale naye kotale wake kuti azitha kuphunzira kunyumba kwao.

## **GAWO LOYAMBA**

### **KUCHOKA KU MDIMA KULOWA MKUWALA**

#### **ZAMKATIMU**

##### **Chiyambi**

**Phunziro 1**..... Zakariya amvera Mulungu

**Phunziro 2**..... Zakariya alankhula

**Phunziro 3**..... Yohane M'batizi

**Phunziro 4**..... Maria adabwa ndi chisankho cha Mulungu

**Phunziro 5** ..... Mulungu alonjeza kukhululukira

**Phunziro 6**..... Mulungu alonjeza kubwezeretsedwa ndi chitetezo

**Phunziro 7** ..... Mulungu alonjeza kutitsogolera m'njira zathu

**Phunziro 8**..... Mulungu alonjeza kuwala mu m' mdima

**Phunziro 9**..... Mulungu alonjeza kupezeka pakati pathu

**Phunziro 10**..... Onse Sali Osankhidwa

**Phunziro 11**..... Kuitanidwa ndi maitanidwe a mzimu woyera

**Phunziro 12** ..... Mulungu asankha osauka

**Phunziro 13**..... Mulungu aitanira anthu ake ku kuunika

**Phunziro 14** ..... Kupereka chiyembekezo mu nthawi ya mtsogolo

#### **CHIGAWO CHACHIWIRI**

### **MULUNGU AKHALA PAKATI PA ANTHU AKE**

**Phunziro 1**..... Mulungu pakati pathu

**Phunziro 2** ..... Thawa choipa.

**Phunziro 3**..... Kwathu kwatsopano

- Phunziro 4** .....Khristu ndi mfumu yathu
- Phunziro 5**..... Khristu atipembedzera
- Phunziro 6**.....Kupemphererana wina ndi nzake
- Phunziro 7** .....Kupereka molowa manja
- Phunziro 8**.....Mulungu wa chilungamo.
- Phunziro 9**..... Phwando lotsiliza.
- Phunziro 10** ..... Kuunika kwa chikondi
- Phunziro 11**..... Kuitanidwa ku chikondi
- Phunziro 12** .....Chimwemwe m'chikhulupiro
- Phunziro 13**..... Kukhululukirana

## **CHIYAMBI**

Mateyu 28:18-20 Yesu mwini akukhazikitsa utumiki [great commission] Ndipo akutsindika kuti mukani, Phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza vesi 20 ndikuwaphunzitsa asunge zinthu zonse. Kotale ndi chida chophunzitsira ndi kuphunzirira, pachifukwa ichi wachinyamata aliyense wayenera kukhala naye wake wake kotale kuti athe kuphunzira bwino pa kalasi komanso kunyumba.

Kotale wathu m'chigawo chino akufotokoza zambiri za kutuluka mu m'dima ndi kulowa ku kuunika kodabwitsa kwa Ambuye wathu Yesu Khristu. Pamene tikuti anthu ambiri amafuna kuwala, zapezeka kuti pali anthu ambiri kuphatikizaponso a chinyamata omwe ali mu m'dima ndipo asowa kuunika kwa Ambuye wathu Yesu kuti atiwalire. Pomwe ife tidzafika ku kuwala kodabwitsa sitidzakhalanso kakasi ndi mavuto omwe akunga dziko la pansi ndi achinyamata lero chifukwa njira ndi mayankho athu tidzawaona mosavuta. Achinyamata dziwaninso kuti sizophweka kuchoka mu m'dima mu dziko lomwe muli mavuto ochuluka komanso pa nthawi yomwe anthu akuchita zinthu mwachisawawa ponamizira kuti ndi ufulu wawo kuteru ayi, izi zisowekanso kuphatikizapo mapemphero apadera m'magulu omwe ife achinyamata timakomana.

Tsogolo la kufalitsa uthenga wabwino ndi kutukula mpingo lili m'manja athu ife achinyamata choncho tisagone koma tiuke kutulo ndi kuyamba kuyenda mkuunika kwa Ambuye wathu Yesu Khristu podzipereka ku ntchito yake., ife eni komanso ndi chuma chathu, nzeru zathu ndi zonse za mkati mwathu.

# PHUNZIRO 1

## ZAKARIYA AMVERA MULUNGU

1<sup>st</sup> July, 2023

Lemba la phunziro: Luka 1:8-20

**Vesi Loloweza:** *Luka 1:13 Koma mngelo anati kwa iye, usaope Zakariya, chifukwa kuti lamveka pemphero lako ndipo mkazi adzabala mwana wamwamuna ndipo udzamutcha dzina lake Yohane.*

### CHIYAMBI

Achinyamata ambiri amavutika ndi chikayiko komanso mantha zomwe zimawayikira malire a chikhulupiriro ndi kuthekera kwawo. Kodi chikayiko ndi mantha zimakhudza bwanji moyo wathu? Achinyamata amataya mwayi wawo wa maphunziro, ntchito, banja, business komanso chitukuko ndi utumiki chifukwa cha mantha ndi chikayiko. Ngakhale panali zotsatira zoyipa chifukwa cha kukayikira ndi mantha a Zakariya koma izi sizidapangitse kuti zichotse chikhumbo khumbo cha Mulungu chokwaniritsa lonjezo lake pa mtundu wa anthu. Choncho mphunziro lathu la lero achinyamata lititengera ku zotsatira za mantha ndi chikayiko chathu pa zomwe Mulungu watikonzera kuti zichitike pa moyo wathu.

### MAFUNSO

1. Kodi ndi chikayiko chanji ndi mantha otani omwe achinyamata timakhala nawo pa moyo wathu? Nanga izi zimakhudza bwanji moyo wanu wa m'tsogolo?
2. Kodi ndime yomwe tawerenga lero ndi yofunika bwanji pakati pa achinyamata lero?
3. Fotokozani ndi kukambirana za chikayiko ndi mantha a Zakariya, kodi kunali koyenera kuti Zakariya akhale ndi mantha?

4. Fotokozani ngati Zakariya anali munthu woyenera kulandira lonjezo la Mulungu, ndipo perekani zifukwa zitatu pa yankho lanu
5. Kodi ndi zoletsa ziti zomwe zimafooketsa chikhulupiriro chathu monga Elisabeti, Sarah, Rakelo, Hanna. Kodi Mulungu amagwiritsa ntchito bwanji nyengo zopanda chiyembekezo kuti aonetse tsogolo lathu lowala?
6. Kodi zotsatira za lonjezo la Mulungu kwa Zakariya ndi Elisabeti zinali zotani? [vesi 14-17]
7. Kambiranani momwe phunziro la lero lingakuthandizireni kugonjetsa chikayiko chanu ndi mantha pa moyo wanu. Nanga zingabweretse bwanji chikhulupiriro chanu posatengera kuti Mulungu sakuyankha mapemphero anu monga momwe inu mukufunira.

## **KUFOTOKOZA**

Zakariya adaoneka wamantha ataona mngelo yemwe anamuonekera zomwe zikhoza kuwachitikira achinyamata ambiri lero lino pokomana ndi mthenga wa Mulungu. Ngakhale Zakariya adapita mkachisi kukapereka msembe ndi kulankhula ndi Mulungu adaoneka wodabwa pamene Mulungu adayankha. Ngakhale mngelo adamulimbikitsa Zakariya koma iye adaonetsabe kukayikira. Ifenso tikadakhala ndi mantha athu tikadakhala ife Zakariya kapena chikayiko chathu.

Zakariya adalandira nkhani yokoma yomwe adayenera kukondwerera popanda mafunso ambiri ndiyo ya kubadwa kwa Yohane mwana wa mu ukalamba wake. Koma Zakariya anali ndi chikayiko chifukwa cha ukalamba wake koma Mulungu sachedwa safulumira koma achita zinthu mu nthawi yake. Kodi zotsatira za chikayiko ndi mantha a Zakariya zinali zotani? Zakariya adakhala wosalankhula kufikira Yohane atabadwa. Kodi ife achinyamata chimabweretsa chikayiko ndi mantha pa moyo wathu ndi chiyani mu utumiki wa Mulungu? Zakariya anali ndi zaka zochulukira koma Mulungu adamuchitira chifundo ndipo anali ndi mwana mu ukalamba wake. Achinyamata ambiri amakhala ndi mantha chifukwa

cha umphawi ulova kapenanso kuchepa kwa maphunziro. Kubadwa kwa Yohane chinali chiyambi cha chipulumutso chathu lero popeza iye adabadwa kudzakonza khwalala la Ambuye wathu Yesu Khristu. Achinyamata ambiri tataya mwai wa business, ntchito, maphunziro chifukwa cha kukayikira ndi mantha pomwe Mulungu akutiwitana. Dziwani kuti Mulungu wathu ndi wa dongosolo

Mau a Yesu woperekedwa kwa ife mawu a mzimu woyera mu zolemba za Luka akutiwiza kuti cholinga cha Mulungu kwa ophunzira ake ndiye kuti akakhale mboni zake kufikira ku malekezero a dziko lapansi [Machitidwe 1: 8] Vesi lili ndi cholinga komanso lonjezo . Monga Zakariya analandira nkhani yabwino kuchokera kwa Mulungu ndipo idasintha moyo wake onse ife tidalandira nkhani yabwino ya Yesu Khristu mwa chisomo yomwe yapulumutsa moyo wathu kwa muyaya

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Achinyamata tisakhale ndi mantha pomwe tikutumikira Mulungu koma tidzipereke kwa thunthu ndipo timutumikire ndi zonse za mkati mwathu kuphatikizapo chuma chathu.

### **MALEMBA OWERENGA KUNYUMBA**

Yohane 10:22-30, Yohane 16 :1-15, Masalmo 103 :1-12, Luka 1:1-25, Yesaya 30:18-26



**ZAKARIYA ALANKHULA**

**Lemba la phunziro:** Luka 1:57-66, 76-79

**Vesi Loloweza:** *Luka 1:76 Eya, ndipo iwetu kamwanawe udzanenedwa mneneri wamkulukulu, pakuti udzatsogolera Ambuye kukonza njira zace.*

**CHIYAMBI**

Pali zinthu zambiri zomwe ife achinyamata timachita ndipo zimabweretsa chiyembekezo cha tsogolo lowala la makolo athu ngakhale ife tomwe. Chitsanzo chabwino chingakhale chiyani? Pamene inu mwasankhidwa kupita ku secondary sukulu kapena ku university makolo amakhala ndi chiyembekezo cha tsogolo labwino la inu monga mwana wawo komanso inu mumakhala ndi chiyembekezo chodzapeza ntchito yabwino. Komanso pamene wachinyamata wapeza banja labwino amakhalanso ndi chiyembekezo cha tsogolo labwino. Kubadwa kwa mwana kumabweretsa kusintha ndi chimwemwe pa khomo komanso m'mudzi. Kodi kubadwa kwa mwana kumabweretsa chiyembekezo bwanji mmudzi? Kubadwa kwa Yohane chinali chiyambi cha kukwaniritsidwa kwa malonjezo a Mulungu pa Zakariya komanso mtundu wonse wa ana a wanthu ku dziko lonse lapansi. Phunziro lathu la lero tiwonanso za chiyambi cha chimwemwe chatu mwa Yesu

**MAFUNSO**

1. Fotokozani za chimwemwe chomwe chidabwera m'banja lanu inu mutabadwa kapena kutabadwa m'mbale wanu.
2. M'chifukwa chiyani kubadwa kwa mwana kumabweretsa kusintha ndi chimwemwe pakhomo kapenanso pa mudzi?

3. Kodi mukuganiza kuti kubadwa kwa Yohane kudabweretsa kusintha bwanji m'moyo wa Zakariya ndi Elisabeti? Nanga kunali kofunika bwanji pa moyo wa okhulupirira a lero, kambiranani.
4. Chifukwa chiyani Mulungu adapangitsa Zakariya kuti asiye kulankhula?
5. Kambiranani, mukuganiza kuti nkhani yoti Elisabeti ali ndi mwana Zakariya anayirandira bwanji? Nanga achibale, mudzi onse kulingalira kuti anali achikulire.
6. Fotokozani momwe inu mumamvera za lonjezo la Mulungu pa moyo wa achinyamata okhulupirira.
7. Tsimikizani kuti Mulungu sachedwa safulumira pa malonjezo ake ndipo ndi okhulupirika
8. Kambiranani za adani a chikhulupiriro nanga mungathane nawo bwanji

## **KUFOTOKOZA**

Kodi inu munayamba mwalonjezedwapo? Eeee mzachidziwikire kuti ambiri a ife tidalonjezedwapo ndipo enanso tidakhumudwapo chifukwa zolonjezedwazo sizidatheke ngakhale tidakonzekera bwino lomwe. Ngakhale Zakariya anali wa msembe koma adakayika atamva lonjezo la Mulungu mwa mzimu woyera kuti mkazi wake adzakhala ndi mwana chifukwa anali anthu a zaka zochulukira. Mukuganiza kuti ichi chinali chifukwa chokwanira kuti Zakariya akayikire lonjezo la Mulungu? Mulungu anamupatsa chizindikiro kuti adzikhala osayankhula kufikira mwanayo atabadwa. Achinyamata a lero timafuna chizindikiro kapenanso kuyesera kuti tikhulupirire zomwe mau a Mulungu akutiya ndipo ena adagwa nazo mu misampha yoyipa. Ena adalephera sukulu chifukwa atawuzidwa kuti kukhala ndi zibwenzi pomwe uli ku sukulu sizabwino ndipo pofuna kuyesera adatenga pathupi ndipo maphunziro awo adathera pa njira.

Lonjezo la Mulungu loti Zakariya adzakhala ndi mwana silinali lake lokha komanso la dziko lonse la pansi popeza limabweretsa

chiyembekezo cha kubadwa kwa ambuye wathu yesu Khristu. Malonjezo a Mulungu anakwaniritsidwa. Chozizwa ichi kuti Elisabeti anakhala ndi mwana Yohane mbatizi tikuona Mulungu akusunga ndi kukwanitsa lonjezo lake ku mtundu wa anthu. Kuyambanso kuyankhula kwa Zakariya tikuonanso ubwino wa Mulungu pa Zakariya kuti Mulungu akugwira ntchito ndi Zakariya kulengeza za kubadwanso kwa Yesu Khristu.

Zozizwa izi zikutikumbutsa ife chikondi cha Mulungu chomwe ali nacho pa anthu ake ndi chipulumutso chodabwitsa chomwe Mulungu anachitira anthu ake. Mulungu akutionetsera ife kuti tikakhulupirika pamaso pake iye adzakwaniritsa malonjezo ake pa ife.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu ali ndi dongosolo lake lopulumutsira mtundu wa anthu ndipo sachedwa safulumira ife tikhale okhulupirika nthawi zonse.

### **MALEMBA OWERENGA KUNYUMBA**

Malaki 3:1-18, 2 Petro 1:16-21, Zakariya 12 :1-10, Luka 1:57-80;  
Malaki 4: 1-6

**YOHANE MBATIZI**

**Lemba la phunziro:** Luka 3:2-6, 15-18

**Vesi Loloweza:** *Luka 3:3 Ndipo iye anadza ku dziko lonse la m' mbali mwa Yordano, nalalikira ubatizo wa kulapa mtima kuloza ku chikhululukiro cha machimo.*

**CHIYAMBI**

Achinyamata amafuna munthu wa mphamvu komanso wa ulamuliro yemwe akhoza kuwalamulira ndi kuwatsogolera pa moyo wawo. Izi zapangitsa achinyamata ndi anthu ambiri kutsatira anthu a ndale omwe akuganiza kuti ali ndi ulamuliro komanso mphamvu zochuluka m' dziko. Taganizirani nthawi ya kampeni misonkhano ya a ndale imadzadza ndi achinyamata ochuluka omwe alibe chiyembekezo koma kuyembekezera atsogoleri a ndalewo kuti iwo akadzakhala olamulira adzawapezetsa mwayi wa ntchito, ngongole ndi malonda ndi kuti iwo adzamasulidwa mu ukapolo wa umphawi. Kodi mtsogoleri otere angapezeke kuti?

Phunziro lathu la lero Yohane m' batizi akulalikira nkhani yabwino ya m' tsogoleri yemwe ali ndi mphamvu zochuluka ngakhale kuposa iye mwini yemwe akudza ndipo adzabatiza ndi mzimu woyera ndi moto. Chinali chosavuta kwa Yohane kunena kuti yemwe akudza pa mbuyo pake ndi wamphamvu kuposa iye, chifukwa anazindikira za ntchito yomwe amayenera kugwira. Inu achinyamata ntchito yanu ndi yotani pa mpingo wanu.

**MAFUNSO**

1. Taganizani za anthu awiri pa mpingo panu omwe amayankhula ndi ulamuliro, ndipo winayo mumamusilira koma winayo ayi.
2. Kodi Yohane m' batizi anakwaniritsa bwanji ulosi wa Yesaya?

3. Kodi ndi utumiki uti wa Yohane m'batizi unamulumikizitsa iye ndi ulosi wa m'chipangano chakale?
4. Kodi cholinga cha ubatizo wa Yohane m'batizi chinali chiyani? Nanga lero anthu ubatizo amaumvetsa motani?
5. Kodi Yesu adayeneranso kubatizidwa? Kunali kofunika bwanji kuti Yohane amubatize Yesu?
6. Fotokoza kusiyana kwa ubatizo wa Yesu ndi wa Yohane molingana ndi zomwe Yohane adanena.
7. Kodi Yohane adayankha bwanji pomwe anthu amkadabwa ngati Yesu analidi mpulumutsi. Nanga izi zikufotokoza chiyani za khalidwe la Yohane m'batizi
8. Kambiranani zomwe tingaphunzire za utsogoleri ndi kutumikira kuchokera kwa Yohane

### **KUFOTOKOZA**

Achinyamata ngakhaleonso anthu onse amafuna atsogoleri abwino ngakhale iwo amene ali atsogoleri amayang'ana anthu omwe ali atsogoleri abwino. Pomwe tikukomana ndi Yohane M'batizi kumayambiriro a buku la Luka mutu 3 tikuona m'tsogoleri yemwe anayamwa chidwi cha anthu ochuluka. Khwimbi la anthu linasonkhana kudzamvera iye ndi kulandira ubatizo wa kulapa. Koma utumiki wa Yohane sunali mathero a zonse. Yohane analikonzekeza anthu ku utumiki wa uthenga wabwino. Kodi ife achinyamata timawakonzekeretsa bwanji anzathu ku utumiki wa kulapa ndi kutembenuka mtima?

Nthawi zambiri pamene achinyamata apsinjika ndi mavuto adziko lapansi monga umphawi, usiwa, ulova, kusowa kwa chikondi, umasiye ndi mavuto ena ambiri amasowa kulandira uthenga wa chiyembekezo kuchokera kwa achinyamata anzawo. Koma tikhoza kuona kuti chifukwa cha kusoweka kwa uthenga wa chilimbikitso achinyamata ambiri adzimangirira ndi kutaya miyoyo yawo. Chinanso chomwe tikuonapo ndi kukhala ndi utsogoleri wodzichepetsa, kuti ngakhale

anthu ambiri anabwera kudzamvera mau ake koma iye adawaunza momveka bwino kuti pali wina yemwe akubwera ndipo iye ali woposa.

Anthu ena ayeserapo kupereka zinthu kapena uphungu ooneka ngati thandizo koma lisali thandizo chifukwa chosafuna kudzichepetsa kwa anthu ena koma Yohane akuti pali wina wondiposa yemwe akubwera. Yesu ndiye mwini wa ulosi ndi uneneri onse omwe unalipo kuyambira chipangano cha kale ndipo Yesu atabwera anakwaniritsa ma ulosi ndi ma uneneri onse ndipo kwa ife achinyamata tayenera kulimbikitsa kuchita mau a Mulungu modzichepetsa monga Yohane M'batizi.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Tiyeni tidzichepetse ndipo Mulungu adzaticweza.

### **MALEMBA OWERENGA KUNYUMBA**

Yohane 1: 29-42; Yohane 1: 1-51, Yesaya 40:1-11, 21-31, Luka 3 :2-18

**MARIYA ADABWA NDI CHISANKHO CHA MULUNGU**

**Lemba la phunziro:** Luka 1:46-55

**Vesi Loloweza:** *Luka 1:46 Ndipo Maria anati; Moyo wanga ulemekeza Ambuye.*

**CHIYAMBI**

Anthu amatha kusankhidwa kukhala atsogoleri potengera mphamvu zawo, chuma chawo ndi ulamuliro wawo. Kodi ife tayenera kuyang'anira chiyani pomwe tikusankha anthu kuti akhale atsogoleri athu? Malingana ndi bukhu la Luka Mariya anasankhidwa kudzakhala Mai wake wa Yesu kutengera kudzichepetsa komwe anali nako. Inu achinyamata mumafuna kuti atsogoleri anu akhale wotani? Kukhala wodzichepetsa sichinthu chapafupi pakati pa achinyamata maka m' masiku athu ano. Pomwe akuti Maria anali namwali izi zikupereka chiyembekezo kuti Maria sanali wokalamba koma wachichepere yemwe anadzichepetsa nasunga unamwali wake. Kodi Yesu akadati abadwe lero akadapezeka namwali woti Yesu abadwiremo? Phunziro lathu la lero lititengera koonna chitsanzo cha Maria monga m'tumiki wodzichepetsa.

**MAFUNSO**

1. Fotokozani njira zomwe timatsata pofuna kusankha anthu kuti tiwayike m'maudindo wosiyana siyana.
2. Kambiranani chomwe chinapangitsa Maria kuyimba nyimboyi ndipo tchulani zinthu zomwe Maria adayamikira Mulungu m'nyimboyi
3. Kodi ndi mau ati a Maria omwe akutsimikiza kudzichepetsa mtima kwa Maria?
4. Kodi Maria adamufotokoza bwanji Mulungu poyimba nyimboyi.
5. Tsimikizani kuti Yesu adangoyenera kubadwira kwa Maria.

6. Mukuganiza kuti m'chifukwa chiyani akhristu [achinyamata] ambiri amavutika kuti awonetse mtima wodzichepetsa weniweni.
7. Fotokozani zomwe achinyamata tingaphunzire kuchokera ku chitsanzo cha Maria kuti zitithandize kukula mu uzimu?

## **KUFOTOKOZA**

Mulungu amasankha anthu pa ntchito zosiyana siyana potengera ndondomeko zake za Iye mwini. Ngakhale kuti ife timasankha anthu potengera nzeru ndi luntha lawo, maonekedwe awo, chuma chawo, kutchuka kwawo, koma baibulo lidalemba za Mulungu kusankha anthu omwe dziko lapansi silikadawasankha. Izi zikutiphunzitsa kuti kudzichepetsa ndi mbali imodzi ya maziko a moyo wa chikhristu. Monga momwe Maria anadabwira kuti Mulungu adamusankha iye ku ntchito yofunika chotere ife tayenera kudabwa ndi chikondi cha Mulungu pa ife kuti anatumiza mwana wake kuti ife tikhale ndi moyo. Nyimbo ya Maria ndi chitsanzo chabwino kwa ife cha kuyamika ndi kuthokoza Mulungu. M'mene ife timachitira ndi uthenga wabwino ndi kuti Mulungu anatisankha ife kwa iye yekha, tayeneranso kudziwa mtengo wake wa mwana wake ku chiombolo chathu.

Ifenso tili ndi nyimbo yomwe tayenera kuyimba chifukwa cha chiombolo cha Yesu chomwe Mulungu watipatsa. Tayeneranso ife achinyamata kuonetsa uthenga wabwino momwe tikukhalira ndi anthu ena, mmenenso tikutumikilira anthu ena omwe atizungulira.

Izi zikutanthauza kuti pa mpingo wathu munthu aliyense, udindo uliwonse, ndi utumiki uliwonse wayenera kudzichepetsa ndi kulemekeza Mulungu mu utumiki wawo. Mukhoza kukhala ndi udindo waukulu kapenanso kukhala munthu wodziwika ndi wotchuka pa mpingo panu kapena mmudzi mwanu, Mulungu watiyitana kuti timutumikire ndi kudzichepetsa mtima konse ndi khumbo lofuna kulemekeza Iye .



## **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu sayang'ana nkhope akafuna kusankha munthu mu ntchito iliyonse ndipo amafuna kuti tigwire ntchito yake modzichepetsa mtima ndi kudzetsa ulemerero ku ntchito yakeyo

## **MALEMBA OWERENGA KU NYUMBA**

Mateyu 1:18-25, Yesaya 9:1-7, Yesaya 11:1-10, Luka 1:26-55

**MULUNGU ALONJEZA KHULULUKIRA**

**Lemba la phunziro:** 2 Mbiri 7:12-22

**Vesi Loloweza:** *2 Mbiri 7:14 Ndipo anthu anga otchedwa dzina langa, akadzichepetsa nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zawo zoipa pamenepo ndidzamvera m'mwamba ndikukhululukira zoipa zawo ndi kuchiritsa dziko lawo.*

**CHIYAMBI**

Mmene anthu tili kuno kudziko la pansi tili ndi maubale osiyanasiyana ndipo anthu amapanga maubale amenewa pa zifukwa zosiyanasiyana. Ndi maubale ati omwe ife achinyamata timapanga m'magulu athu? Ubale umakhudza kuchitirana zabwino, kudalitsana wina ndi m'nzake, kukhala ndi chiyembekezo komanso zotsatira. Kodi ife achinyamata timalemekeza bwanji ndi kusunga maubale athu? Pamene Mulungu analengeza kuti kachisi wa Solomoni ndi nyumba yake, ulemu umenewu udabwera ndi malonjezano ake. Muphunziro lathu la lero tionamo malonjezo a Mulungu pa kachisi wake.

**MAFUNSO**

1. Tchulani madalitso, chiyembekezo chanu, komanso zotsatira za ubale omwe inu munauona kukhala ofunika kwambiri.
2. Kodi inu mwayenera kuchita chiyani kuti musunge ubale umenewu komanso kusonyeza kuti mumalemekeza ubalewu?
3. Kambiranani mfundo za mu pemphero la Solomoni zomwe zili mu mutu 6. Kodi ndi ziti mwa mfundozi zomwe zikukukhudzani pomwe inuyo mukuona mayankho a Mulungu pa ndime ya lero?

4. Fotokozani zinthu zinayi zomwe ana Aisraeli anayenera kuchita kuti Mulungu abwezeretsenso ubale wake ndi anthuwa atakira Mulungu mu vesi 14.
5. Kodi inu mungafotokoze bwanji zomwe zinachitika m'mbiri ya Aisraeli ndi kachisi utatha ulamuliro wa Solomoni poyang'ana malonjezo ndi machenjezo a Mulungu mu vesi 16, 22?
6. Mu nthawi yathu ino ndi milungu iti yomwe ilipo ndipo timayesedwa motani kuti tiyipembedze ndi kuyitumikira? Nanga zimakhudza bwanji ubale wathu ndi Mulungu?
7. Fotokozani momwe tingasiyire milungu imeneyi ndi kubwerera kwa Mulungu wathu kuti tikonzenso ubale wathu.

## **KUFOTOKOZA**

Choyamba Mulungu anamuza Solomoni kuti wamva pemphero lake kusonyeza kuti Mulungu anasunga ubale wake omwe unali ubale wa lonjezo. Tikuonanso kuti mapemphero a Solomoni anayankhidwa ndi chitsimikizo choti Mulungu wadzisankhira kachisi wake monga malo a nsembe [vesi 12] A nayikamo zonse dzina lake ndi kupezeka kwake monga malo ake opatulika kuperekeramo nsembe kwa Mulungu.

Mundime yathunso ya lero tikuonanso pangano lopanda malire ndi lonjezo lomwe Mulungu anapanga ndi kholo la Solomoni Davide likukwaniritsidwa. Achinyamata dziwani kuti zomwe munthu umadzala ndi zomwe umakolora ndipo ngati sukolora iwe mwini wake mbewu yako dziwa kuti adzukulu ako ndi omwe amadzakolora, m'chifukwa chake lero tikuona mfumu Solomoni akukolora zomwe kholo lake Davide adafesa. Mulungu akutsimikiza kuti adzaweruzana anthu ngati sachita zinthu zinayi izi kuti akhululukidwe zochimwa zawo.

- Kudzichepetsa
- Kupemphera
- Kufuna nkhope ya Yehova
- Kusiya zochimwa zawo

Mavesi a 17, 18 akulankhula mwa chindunjii kwa Solomoni ndipo ma vesi a 19 mpaka 22 akuchenjeza anthu onse za zomwe zidzachitike ngati sabwerera kwa Mulungu ndi kuleka zoipa zawo. Akusonyezzeratu kuti padzakhala zotsatira zoipa zoopsa ngati anthu sasiya machimo awo. Akuti adzazulidwa ndipo kachisi wawo adzaonongedwa .

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu amasunga malonjezo ake ndipo amakwaniritsa

### **MALEMBA OWERENGA KUNYUMBA**

Deuteronomo 30:1-20, 1 Yohane 1:1-10, 1 Yohane 2 :1-11, 1 Yohane 3:1-10, 2 Mbiri 7 :1-22

**MULUNGU ALONJEZA KUBWEZERETSEDWA NDI  
CHITETEZO****Lemba la phunziro:** Yesaya 43: 1-12

**Vesi Loloweza:** *Yesaya 43:1 Koma tsopano atero Yehova amene anakulenga iwe Yakobo ndi iye amene anakupanga iwe Israeli, usaope, chifukwa ndakuombola iwe ndakutchula dzina lako iwe uli wanga.*

**CHIYAMBI**

Achinyamata timakomana komanso kulimbana ndi zovuta zochuluka zomwe zagwira dziko lapansi. Pakati pathu pali mavuto monga a umphawi, ulova, matenda, maubwenzi osakhazikika maudani, umasiye, kusowa ndalama zolipirira maphunziro awo ndi mavuto ena ambiri. Kodi achinyamata tingapeze bwanji chiyembekezo cha tsogolo labwino pakati pa mavuto ngati amenewa? Phunziro lathu la lero Yesaya akutikumbutsa kuti ngakhale nyengo zathu zitafika povuta bwanji koma Mulungu amapereka thandizo ndi chiyembekezo chabwino. Mulungu amasamalira anthu ake ngakhale atakomana ndi mavuto osowetsa mtendere ndipo Mulungu amasunga pangano lake pa anthu ake. Kodi ife ndife ana a Mulungu? Muphunziro ili tionanso momwe Mulungu amachitira ndi ana ake munthawi ya m'sautso zawo.

**MAFUNSO**

1. Kambiranani za nyengo zomwe inu Achinyamata mumakhala kakasi kusowa mtengo wogwira? Chimapangitsa inu kumva kuti mulibe chiyembekezo ndi chiyani?
2. Fotokozani zovuta zomwe ana a Israeli anakomana nazo mu nthawi yomwe Yesaya amalemba bukhuli?

3. Kodi mau a Mulungu kudzera mwa Yesaya adapereka chiyembekezo bwanji ngakhale kuti samalonjeza kukhala nawo mu nyengo yomwe iwo amadutsamo?
4. Fotokozani malonjezo ena omwe Mulungu anapereka kwa ana a Israeli mu ndimeyi nanga mukuganiza kuti malonjezo amenewa amapereka chitonthozo kwa Israeli?
5. Kambiranani m'chifukwa chiyani achinyamata amaopa zinthu zosaoneka? Ngakhale kuti Mulungu akulonjeza kukhala nafe mu nyengo zonse.
6. Kodi ndi nyengo ziti zoonekeratu zomwe Mulungu amatipulumutsa komanso kupereka chiyembekezo pomwe ife tasweka mtima.
7. Fotokozani ubwino wokhulupilira Mulungu mu nyengo zathu zonse maka ife achinyamata.

## **KUFOTOKOZA**

Ana a Israeli akachimwa Mulungu anali kuwapereka m'manja mwa adani awo monga chilango. Choncho ana a Israeli atakhala m'dziko la chilendo monga akapolo zaka zochuluka anataya chikhulupiriro kuti tsiku lina adzabwerera kwawo. Nthawi zina ifenso achinyamata timataya mtima kuti zathu zidzayenda bwino tsiku lina. Taganizirani za munthu wina yemwe wakhala akudwala kwa zaka zisanu osachira chiyembekezo chake chimakhala chotani?

Mu vesi 2 akuwakumbutsa ana a Israeli zomwe zinachitika pomwe amaoloka Nyanja yofiira komanso mtsinje wa Yordano pofuna kuwakumbutsa kuti Mulungu sawayiwala ngakhale akuyenda m'mavuto zomwe zinachikanso m'buku la Daniel mutu 3 pokamba za Shadreck, Misheki ndi Abedinego.

Mu vesi 5 mpaka 7 akukamba za chikondi choposa cha Mulungu kuti ngakhale ana a Israeli anali ku chibalaliko koma iye adzawabwezeretsanso. Mneneri Yesaya akukamba za lonjezo la

Mulungu lakuti “ bwerani nawo ana anga amuna ndi akazi kuchokera kutali yense wotchulidwa ndi dzina langa’ vesi 6-7. Mau akuti pangano [convenant] anagwiritsidwa ntchito ndi chitsimikizo cha Mulungu kuti litikumbutse umulungu wosatha ndi wa muyaya yemwe anadziulura yekha kwa Mose m’chitsamba chonyeka chija. Nthawi ya Mulungu ndi yokoma nthawi zonse chifukwa amapanga zinthu mu nthawi yake ndipo ife achinyamata tisathamangire zinthu zomwe sizathu komanso tisataye mtima kuti Mulungu watiyiwala ayi popeza iye sazengereza nalo lonjezano lake.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu wathu ali wokhulupirika nthawi zonse ndipo iye ndiye chiyembekezo chathu nthawi zonse

### **MALEMBA OWERENGA KUNYUMBA**

2 Atesalonika 3:1-17, Yesaya 42:14-28, Ezeieli 37:1-28, Yesaya 43:1-13, Hoseya 11

**MULUNGU ALONJEZA KUTITSOGOLERA**

**Lemba la phunziro:** Yesaya 48:1-8, 17

**Vesi Loloweza:** *Yesaya 48:17 Atero Yehova mombolo wako, woyera wa Israeli, Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndikuphunzitsa kupindula, amene ndikutsogolera m'njira yoyenera iwe kupitamo.*

**CHIYAMBI**

Salmo 23 likuyamba ndi kuti” Yehova ndiye mbusa wanga sindidzasowa” Anthu akale anali kuweta nyama zosiyana siyana pa zifukwa zosiyanso , ndipo abusa woweta nyamazo amakhala pa ntchito yaikulu ndi yolemetsa. Ngakhale kuti lero chimamveka monyozeka katchedwa m’busa koma anthu awa anali wofunika ndipo kukhala m’busa wabwino mwazina zimatanthauza kudzipereka kwa thunthu ngakhale kutaya moyo kumene chifukwa chofuna kupulumutsa nkhosa. Yesu ndiye m’busa wabwino ndi wamkulu, chikondi chake ndicho chopanda malire ndi msembe yake sinangomutengera moyo wake wokha komanso kutenganso machimo onse, m’dima ndi ululu wa dziko lapansi. Adalekanitsidwanso ndi atate ake kuchoka kumwamba. Adachita zonsezi chifukwa cha chikondi chenicheni pa ife monga nkhosa za pa busa pake. Anthu amafuna kuona zinthu za m’tsogolo kapena zomwe iwo adzakhale m’tsogolo. Yesaya akuti ndi Mulungu yekha yemwe amadziwa za m’tsogolo ndi kuziululira izi kwa ana a Israeli ngakhale iwo anali anthu osamvera Mulungu

**MAFUNSO**

1. Kodi ndi zinthu ziti m’dera lathu zomwe zimasonyeza kuti anthu amafuna atadziwa za m’tsogolo?
2. Kodi inu mukuganiza kuti anthu atadziwa zinthu za m’tsogolo zingapangitse kuti asinthe njira zawo? M’chifukwa chiyani mukuganiza chotero?



3. Perekani zitsanzo za m'baibulo zomwe Mulungu amawauza anthu kapena kuwachenjeza zinthuzo zisadachitike.
4. Fotokozani m'chifukwa chiyani Mulungu anali kuwauziratu anthu zinthu zisadachitike
5. Fotokozani zomwe Mulungu adawachitira, akuwachitira ndi zomwe adzawachitire anthu ake malingana ndi vesi 6-7
6. Kambiranani Mulungu adzatitsogolera bwanji mu njira zathu?
7. Kodi ife tingamupembedze bwanji Mulungu pofuna kulemekeza mfundo yoti Mulungu adzakhala m'tsogoleri wathu?
8. Mau akuti “**m'busa**” amatanthauza chiyani m'moyo wanu?

## **KUFOTOKOZA**

Mundime yathu ya lero Mulungu akupitiriza kuyankhula ndi anthu ake kudzera mwa m'neneri Yesaya. Munthawi ya uneneri wa Yesaya mafumu anai analamulira Yuda. Mafumu atatu Uziya, Hezekiya, ndi Josan anayesetsa kuchotsa anthu ku chipembedzo cha mafano zomwe anayamwira kuchokera ku mtundu wa akanani. Koma mfumu Ahazi anapotoza anthu kuchokera ku kupembedza Mulungu wa kumwamba ndi kumapembedza mafano ngakhale kupembedza mulungu wa ma Asuriya. Monga momwe tichitira achinyamata a lero takopera machitidwe achilendo mkuchokera ku zipembedzo zina ndi kuyiwala kuchita chifuniro cha Mulungu.

Mulungu akukumbutsanso anthu ake kuti Iye ali okhulupirika kwa thunthu kwa anthu ake. Kwa zaka zochuluka Mulungu wakumbutsa anthu za ku khulupirika kwake komanso dongosolo lake lopulumutsira iwo kwa adani awo. Tikaona kulephera kwa anthu pamaso pa Mulungu yemwe anawakonda tikhoza kudabwa kuti m'chifukwa chiyani anthu amenewa anasankha kusamvera Mulungu chotere. Kodi ife timamvetsa ndi kukhulupirira kuti Mulungu alinafe cholinga pa moyo wathu komanso tsogolo lathu.

Baibulo linalembedwa kuti lipereke chitsogozo cha moyo wathu ndi Mulungu wathu komanso kutitsimikizira kuti Mulungu sataya anthu ake ngakhale atakhala kuti akudutsa m'mavuto ochuluka. Ana a Israeli kupezeka ku ukapolo sanali mathero a moyo koma kuti akaphunzire kulemekeza Mulungu yemwe anawalenga ndi kusiya njira zawo zoipa. Mafumu a dziko lapansi amatha kutitsogolera komanso kutisokoneza koma lero Mulungu akulonjeza kuti Iye adzatitsogolera ku choonadi chonse. Pakuti atero Yehova mumbolo wako woyera wa Israeli ndine mbuye wako yemwe ndikuphunzitsa kuti zikuchitire ubwino yemwe atsogolera iwe njira yako Yesaya 48:17

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Ife tivomereze kuti dzanja la Mulungu lipitilize kutitsogolera komanso tidzichepetse ndi kudalira pa Mulungu yekha basi.

### **MALEMBA OWERENGA KU NYUMBA**

Masalimo 119:81-96, Masalmo 23, Miyambo 3:1-15, 1Petro 1:3-25,  
Yesaya 48:1-22

**MULUNGU ALONJEZA KUWALA MU MDIMA**

**Lemba la phunziro:** Yesaya 58:6-10

**Vesi Loloweza:** *Yesaya 58:10 Ndipo ngati upereka kwa wanjala chimene moyo wako umakhumba ndi kukhutitsa moyo wovutidwa pomwepo kuunika kwako kudzauka mu mdima ndipo usiku wako udzanga usana.*

**CHIYAMBI**

Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi . China mwa zomwe zinalengedwa zinali kuwala ndi m'dima. Ntchito zambiri zabwino zimachitika m'kuwala ndipo ntchito zambiri zoipa zimachitika mum'dima. Kukhala mu m'dima ndi chinthu chomwe anthu ambiri sakonda kukhalamo pozindikira kuti muli zambiri zomwe zimapereka chiopsezo ku moyo wathu. Ana a Israeli anakhala mu m'dima ku nthawi zambiri pomwe iwo analibe chiyembekezo kuti Mulungu adzakhalanso thandizo lawo popeza anakhala m'dziko la ukapolo kwa zaka zochulukira . Nthawi zina ife achinyamata timakhalanso mu m'dima wa dzaoneni pomwe mavuto amakunga moyo wathu osadziwa chomwe tayenera kuchita kuti nyengo za moyo wathu zisinthe ndi kukhala pa bwino. Phunziro lathu la lero Mulungu akulonjeza kupereka kuwala kwa iwo omwe ali mu m'dima.

**MAFUNSO**

1. Kodi ndi mawu ati mu ndime yomwe tawerengayi omwe akusonyeza kuti Mulungu sanakondwe mu vesi 1 ndi 2
2. Fotokozani ntchito za atsogoleri. Muganiza kuti m'chifukwa chiyani Mulungu sadakondwe ndi utsogoleri wa nthawi ya ana a Israeli?
3. Inu mukuganiza kuti chinali cholakwika ndi chiyani ndi atsogoleri amenewa kuti asale?
4. Fotokozani miyambo yomwe mpingo umachita lero imene ilibe tanthauzo kapena imachitika ndi zolinga zoipa.

5. Kodi Mulungu anafotokoza bwanji za kusala koyenera ndi kovomerezeka pa maso pake vesi 6-7?
6. Mundime yathu ya lero ndi mau ati akufuna kufotokoza madalitso a Mulungu?
7. Fotokozani zomwe ife tayenera kusintha m'moyo wathu kuti tilandire madalitso a Mulungu ndikubwezeretsa ubale wathu ndi Mulungu.
8. Kambiranani za kuwala komwe kumabwera m'moyo wathu ndipo moyo wathu umasintha ife mkumamva kukoma monga akhristu.

## **KUFOKOTOZA**

Mundime yathu ya lero Mulungu akumutuma m'neneri Yesaya kukadzudzula atsogoleri okhazikika a chiyuda. Iwo amachita zinthu zabwino ndithu pa chipembedzo, mapemphero kupereka nsembe kusala kudya, koma mitima yawo sinali mu chipembedzo. Mulungu anakhumudwa nawo ndipo anamutuma Yesaya ndi uthenga wamphanvu kuti akawadzudzule. Aliponso achinyamata ambiri lero omwe ali a machawi pa chipembedzo koma mitima yawo ili kutali ndi Mulungu. Iwo amachita izi pongofuna kupeza phindu la iwo eni koma mphamvu ya Mulungu anaikana. Achinyamata odziwa kuyimba bwino koma ntchito zawo zili za ku midima. Enanso a ife sitidziwa kupereka zopereka zathu molongosoka pamaso pa Mulungu. Mpingo wa Mulungu lero ukufuna achinyamata odzipereka ndi mtima onse kuti agwire ntchito yabwino.

Kukonderedwa ndi madalitso a Mulungu sikuti zimangobwera mophweka ayi. Malingana ndi ndime yathu madalitso a Mulungu amaperekedwa kwa iwo omwe mitima yawo imathandiza ena mosadzikonda kumbukirani pa machitidwe 20:35 akuti kupatsa kutidalitsa koposa kulandira. Mulungu amayang'ana mitima yathu zomwe zingatiyenereze ife kukhala atumiki a Mulungu okhulupirika

Ndimeyi ikumalizanso ndi kuika ndandanda wa ubwino ndi zotsatira za kuchita chifuniro cha Mulungu monga;

1. Kuwala mu uzimu

2. Kutsogoleredwa mwa chisomo cha Mulungu
3. Kukwaniritsidwa
4. Mphamvu

Izi ndi zomwe Mulungu akulonjeza kwa iwo akumumvera ndi kutsatira chifuniro chake. Madalitso otsiliza analonjezedwa kwa iwo akutsatira mau ake anali kulandira cholowa cha Mulungu. Pomwe Mulungu akulonjeza kuwala mu m'dima ife achinyamata tayenera kumvetsa utumiki wa Mulungu wathu komanso kutsatira choonadi cha mau ake.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu sayiwala anthu ake koma akufuna ife atsogoleri tichite chilungamo pakati pa anthu onse

### **MALEMBA OWERENGA KU NYUMBA**

Aefeso 5: 1-20, 1 Yohane 3:14-24, Yesaya 60:1-8, 58:1-14, Yohane 8:12-20, Masalmo 119:97-112

**MULUNGU ALONJEZA KUPEZEKA**

Lembala phunziro: Yoweli 2:18-31

**Vesi Loloweza:** *Yoweli 2:27 Ndipo mudzadziwa kuti ine ndili pakati pa Israeli ndi kuti ine ndine Yehova Mulungu wanu, palibe wina ndi anthu anga sadzachita manyazi nthawi zonse.*

**CHIYAMBI**

Nthawi zina achinyamata timamva kuti ndife amasiye maka munthawi zomwe tikufuna thandizo koma silikuppezeka pafupi pathu. Nthawi zinanso anzathu omwe timaganiza kuti akhoza kukhala thandizo lathu amatithawa ife mkukhala kakasi opanda mtengo ogwira. Iyi ndi nthawi yomwe achinyamata ambiri amachita khalidwe losakhala bwino monga kumwa mowa, kuchita uhule kusuta fodya, kugwirira amayi komanso ena adangoona kuti kuno sikudziko labwino kukhalako ndipo iwo adangodzipha. Kodi ndimavuto ati omwe angapangitse achinyamata kuganiza motere? Kodi dziko lapansi ndi miyoyo ya anthu idzakhalanso yabwino kusiyana ndi momwe ilili lero? Apa mpomwe pamasowekera mau a mphamvu achilimbikitso kusonyeza kuti alipo wina yemwe amasamala za ife ndipo ali okonzeka kukhala thandizo lathu. Mu phunziro lathu la lero, Mulungu akulonjeza kubwezeretsa zonse zomwe zidaonongeka chifukwa cha munthu ndikubweretsanso mtendere.

**MAFUNSO**

1. Kodi ndi umboni wanji omwe ukusonyeza kuti dziko laonongeka chifukwa cha zochita za munthu. Nanga pali chiyembekezo chanji kuti likhoza kubwereranso?
2. Kodi vesi 18 ikufotoza bwanji za maganizo a Mulungu ndi kudzipereka kwake ku mtundu wa Yuda?

3. Fotokozani madalitso omwe Mulungu analonjeza kwa anthu ake mu vesi 21-27.
4. Kambiranani chomwe chinapangitsa Mulungu kupanga malonjezo amenewa.
5. Fotokozani za ndime zina m'baibulo zomwe zikufotokoza za kubwera kwa mzimu woyera vesi 28-29. Nanga zimenezi zingathe kuwachitikiranso anthu a Mulungu lero?
6. Kambiranani za njira zomwe ife tingatsate kuti tikonzenso ubale wathu ndi Mulungu monga mpingo, m'moyo wathu, m'dziko lathu,
7. Fotokozani momwe uchimo umakhudzira kakhalidwe kathu ka pakhomo, m'mudzi, m'dziko komanso zachilengedwe zina.

## **KUFOTOKOZA**

Utumiki wa Yoweli ukuyamba ndi kulengeza kuti dzombe , dzombe, dzombe likubwera. Dzombe limalumikizana ndi kubwera kwa chiweruzo ndipo limatengedwa monga mliri [Eksodo 10:1-20. Kufika kwa dzombe kunali kutanthauza mavuto pa Israeli komanso chionongeko. Pamene chiweruzo cha Mulungu chili cholungama komanso choyera koma Mulungu ali wachifundo wosakwiya msanga ndi wachisoni. Yoweli 2:13. Mulungu amakonda anthu ake ndipo mwansanje amafunitsitsa kuti awapatse zinthu zabwino zomwe iye akhoza kupereka. Ngakhale atalengeza chionongeko cha anthu ake ndi malo omwe. Mundime yathu ya lero akulonjeza kubwezeretsanso zinthu zonse zomwe zidaonongeka. Cholinga cha Mulungu ndi kupanganso ubale ndi anthu ake.

Ife achinyamata pali nthawi zambiri zomwe timasiyana naye Mulungu pazifukwa zosiyanasiyana mwina chifukwa cha anzathu komanso kusowa kwa chiyembekezo cha tsogolo la bwino. Taganizani ndi njira ziti zomwe zimapangitsa ife achinyamata kusiyana ndi Mulungu? Ena anayamba kuledzera ndipo amamva kuti sangakhalenso bwenzi la Mulungu, ena kusuta, kukhala moyo wa uhule , kuba, kusapita ku mpingo, mwano ndi zina zotero koma Mulungu akulonjeza kuti adzakhala nafe nthawi zonse.

Nthawi zambiri achinyamata chimativuta ndi kuvomereza kuti tachimwa ndipo tisowa chifundo cha Mulungu. Mulungu ali okhulupirika ndipo ngakhale Israeli anachimwa kwambiri pamaso pake koma Iye sanawasiye koma anasungabe pangano kuti sindidzakusiya, sindidzakutaya. Phunziro lathu lero lititengere ku chilimbikitso kuti ngakhale nyengo zathu zitavuta bwanji koma Mulungu adzakhala nafe nthawi zonse bola ife tikabwerera kwa iye ndi kulapa moona mtima. Chionongeko chimabwera ndi cholinga chimodzimodzi mulili uliwonse Mulungu amautumiza ndi cholinga kuti anthu amudziwe Mulungu ndi kumuopa iye yekha.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu wathu ndi wa chifundo chosatha ndipo adzakhala nafe nthawi zonse.

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Eksodo 33:12-23, 34:5-17, Yoweli 1:1-20, 1Yohane 4:1-21, 5:10-21.



**ONSE SALI OSANKHIDWA**

**Lemba la phunziro:** 1 Akorinto 1:18-31

**Vesi Loloweza:** *1 Akorinto 1:28 Ndipo zopanda pake za dziko lapansi ndi zonyozeka anazisanthula Mulungu ndi zinthu zoti kulibe kuti akathere zinthu zoti ziliko.*

**CHIYAMBI**

Pamene anthu akulingalira zosankha atsogoleri a mpingo, a mudzi, a dziko ngakhalenso a mabungwe amalingalira za anthu omwe ali amphamvu, anzeru, ophunzira bwino, achuma, odziwika komanso otchuka.

Chomwechonso pomwe achinyamata tikusankha oti tidzapange nawo banja, maphunziro, malo okhala, ngakhalenso mpingo umene pali zinthu zambiri zomwe timayang'anira kuti tisankhe bwino ndipo kunena zoonapalibe yemwe amafuna kusankha mphwephwa ya zinthu. Phunziro lathu la lero lititengera kuganiza mosiyana pong'ono ndi momwe Mulungu amaganizira ndi kusankha molumikiza ndi phunziro lathu lapitali kuti Mulungu ali wachilungamo ndi woyera.

**MAFUNSO**

1. Tsimikizani kuti Mulungu ali wa chilungamo ndi woyera
2. Kodi m'chifukwa chiyani timaziphatikiza nzeru, luntha, ndi maphunziro, Kambiranani ngati kuli koyenera kuziphatikiza zinthu zimenezi.
3. Kodi zikutanthauza chiyani kuti "*Mulungu anapusitsa nzeru za dziko lapansi*" vesi 20
4. Kambiranani momwe Mulungu amagwiritsira ntchito zopusa za dziko lapansi ndi zofooka za dziko kuchititsa manyazi anzeru ndi zolimba za dziko vesi 27.

5. Fotokozani chomwe chingatipangitse kuganiza kuti anthu a kwa Akorinto amayang'ana kwambiri nzeru za wanthu kusiyana ndi mphanvu ya Mulungu?
6. Kodi kupachikidwa kwa Yesu pa mtanda kunali kofunika bwanji kwa akhristu
7. Kambiranani ngati zili zoonza kuti anthu ochepa amphanvu ndi a ulemu wawo ndi omwe ali woitanidwa mu ufumu wa Mulungu vesi 26
8. Fotokozani kuti tingatani kuti titsogoze nzeru za Mulungu m'moyo wathu kusiyana ndi kutsogoza nzeru za anthu?
9. Inu mungadzitamandire bwanji mwa Mulungu mu sabata ino?

## **KUFOTOKOZA**

Achinyamata lero timafuna zinthu zabwino ndi zotchuka. Koma sizinthu zonse zili zabwino zomwe Mulungu adazisankha ayi. Komanso sizinthu zonse zomwe ife timazikonda zomwe Mulungu amakondwera nazo ayi . Phunziro lathu la lero Mulungu akuti anapusitsa anzeru a dziko lapansi ndi olimbika a dziko nagwiritsa ntchito zopusa ndi zofooka za dziko kuti akachititse manyazi anzeruwo.

Tisayiwale kuti mutu wathu waukulu mu phunziro lathu tikuyang'ana mau oti kuchoka mu m'dima ndi kulowa kukuwala, Anthu okhala mu m'dima satha kuona bwino zinthu zochitika, choteronso anthu ooneka anzeru ndi oona koma chifukwa ali mu mdima satha kuona. Anthu achuma chawo ndi a maphunziro awo a pamwamba koma zochita zawo zosalongosoka. Ambiri mwa ophunzira a Yesu anali osaphunzira koma analandira uthenga wabwino ndi chikhulupiriro nasankha kumutsatira Yesu. Lero aliponso ena ophunzira omwe amati Mulungu kulibe chifukwa Mulungu nzeru ya dziko lapansi anayipusitsa ndipo kwa iwo imfa ya Yesu ilibe tanthauzo ku moyo wawo.

Tikayang'ananso ku dziko lapansi tiona kuti kuli mipingo yochuluka funso mkumati kodi mpingo woona ndi uti mwa mipingo yonseyi. Mutu

wa phunziro lathu ukutithandiza kupeza yankho ponena kuti si onse ali oitanidwa omwe Mulungu adzawasankhe koma okhawo wochita chifuniro chake. Mulungu ndi wadongosolo komanso wa chilungamo ndipo adzabwezera yense monga mwa ntchito zake.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu sakondwera ndi kuchuluka kwa anthu koma ali wochimwa ayi komanso afuna mitima yolapa ndi yosweka kuti ayichitire chifundo

### **MALEMBA OWERENGA KU NYUMBA**

Masalmo 25:1-15, Mateyu 20:1-16, 2 Samuel 17:1- 29, 1 Akorinto 1:18-31

**KUYITANIDWA NDI MAYITANIDWE A MZIMU WOYERA**

**Lemba la phunziro:** 2 Timoteo 1:3-14

**Vesi Loloweza:** *2 Timoteo 1:13 Gwira chitsanzo cha mawu a moyo amene udawamva kwa ine mwa chikhulupiriro ndi chikondi chimene chiri mwa Khristu Yesu.*

**CHIYAMBI**

Tilipo achinyamata ena omwe tidayitanidwapo ku ma interview. Akhoza kukhala ma interview olowera ntchito kapenanso opezera malo a sukulu ku secondary kapena sukulu ya ukachenjede. Mungakhale ndi chithunzi thuzi cha anthu onse omwe adayitanidwa komanso cha iwo omwe amkafunidwa ndi opangitsa ma interview? Nthawi zambiri anthu oyitanidwa amakhala ambiri kuyerekezaa ndi omwe akufunidwa. Phunziro lathu la lero tiona za mayitanidwe a mzimu woyera. Inu munayamba mwayitanidwapo ku ntchito ya Mulungu. Ambiri timavutika ndi kudzikhulupirira tokha kuti tili ndi kuthekera kochita ntchito yabwino. Tingadziwe bwanji kuti tili ndi zotiyenera kuti tichite bwino m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku? Pamene tayika chikhulupiriro chathu pa Yesu Khristu mpomwe ife timazindikira kuti tikhoza kukwaniritsa zonse opanda vuto chifukwa mthandizi wathu tili naye. Timoteo adamva mayitanidwe a Mulungu m'moyo mwake ndipo izi zidatsimikizika ndi Paulo mu vesi 5 ndi 6. Koma Timoteo amavutika ndi mantha vesi 7. Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha koma kulimbika ndi chikondi. Nthawi zina zimaoneka ndi ndi mwa chikhalidwe kukhala ndi mantha pa ntchito yomwe Mulungu watipatsa maka ife achinyamata. Lero tiona chitsanzo cha Timoteo wachinyamata m'nzathu akusenza ntchito yakutsogolera mpingo wa Mulungu.

**MAFUNSO**

1. Kodi ife tidayamba tapatsidwapo ntchito yomwe ife eni timaona kuti si ife oyenera pa ntchitoyo?

2. Fotokozani chomwe chimapangitsa kuti munthu udzidzikayikira kuti sungakwanitse kugwira ntchito yomwe wapatsidwa.
3. Kambiranani chomwe chikanapangitsa Timoteo kuchita manyazi ndi chiyani mu vesi 8, Nanga zimenezi zikadakhudza bwanji utumiki wake.
4. Kodi vesi 9 ndi 10 likutithandiza bwanji kumvetsa mphamvu ya Mulungu, kambiranani momwe mphamvu ya Mulungu imachotsera manyazi athu ndi mazunzo pa moyo wathu.
5. Fotokozani kufunika kwa mphatso za uzimu pa mayitanidwe athu. Nanga chingapangitse kuti mphatso zathu za uzimu zizilare ndi chiyani?
6. Ngati inu mwakhala mukumva kuti siinu woyenera mayitanidwe a Mulungu phunziro la lero likuthandizani bwanji kuti mudzikhululupirirensa.

## **KUFOTOKOZA**

Timotelo anali kale mu utumiki wa Mulungu pomwe Paulo amamulembera kalata imeneyi kumulimbikitsa. Timaphunzira za Timoteo koyamba, mu Machitidwe a atumwi 16 pamene Paulo adakomana naye ku Lustiko. Timoteo anayamba kukhulupirira ali wamng'ona ndipo Paulo akutsimikiza kuti ngakhale gogo ake anali wokhulupirira. Timoteo anali kuchita bwino mu utumiki ndithu koma chifukwa cha kumangidwa ndi kumzunzidwa kwa Paulo zidampangitsa kukhala ndi chikayiko mu utumiki ndi mayitanidwe ake. Pali zinthu zambiri zomwe zimatipangitsa ife achinyamata kukhala ndi chikayiko pa mayitanidwe athu. Koma Timoteo nkutheka panali zinthu zitatu zomwe zinamupangitsa kukayikira mayitanidwe ake;

1. Timoteo amadziwa chomwe anayitanidwira kukachita koma mkutheka anayang'ana kwambiri umwana wake ndi kusathekera kwake mmalo moyang'ana Mulungu yemwe wamuyitana kuti akagwire ntchito mmalo mwa iye. Pamene Mulungu watiyitana ku

ntchito ina iliyonse tayenera kuyang'ana pa kuthekera kwa Mulunguyo osati kuthekera kwathu.

2. Mkuthekanso Timoteo anapanikizidwa ndi mantha polingalira kuti iye sangakhale ngati monga Paulo mwini. Nthawi zina achinyamata amadzimva kuti sali oyenera poganizira kuti iwo sangafanane ndi anthu ena otchuka amdera lawo kapena pa mpingo pawo. Koma Mulungu sakuyembekeza ife kuti tikhale okopera ena ayi . Dziwani kuti Mulungu anakulengani inuyo monga munthu wapadera-dera komanso ndi cholinga chanu-chanu
3. Mantha a Timotelo opezeka mu vesi 8 mkutheka amabwera chifukwa choopa kuchita manyazi achimzuzo chopezeka mu uthenga wabwino. Ntchito ya Mulungu yomwe ife timagwira sikuti imatipangitsa ife kukhala anthu abwino kwenikweni. Kawiri-kawiri imalimbana ndi umunthu wathu .

Chinthu china chomwe tayenera kuphunzira m'phunziro lathu la lero m'chakuti mayitanidwe anthu sakuperekeratu kuthekera kotu zinthu zonse zidzatiyendera bwino pa moyo wathu ndi kuti zonse zidzakhala zophweka ndi zo pepuka ayi. Komabe chofunika kwambiri ndi kukhulupirira Mulungu kuti atitsogolere nthawi zonse kuchipambano cha mayesero onse.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Amene adatiyitana ife ku utumiki ali ndi mphamvu yakutitsogolera ngakhalenso kutipatsa zipangizo za utumikiwo choncho tisachite manyazi koma kuyang'ana kwa iye nthawi zonse

### **MALEMBA OWERENGA KU NYUMBA**

Yohane 15: 1-14, Agalatiya 4:1-7, Eksodo 19:1-8, Levitiko 19:2-18, 20:2-26

**MULUNGU ASANKHA OSAUKA**

**Lemba la phunziro:** Yakobo 2:1-12

**Vesi Loloweza:** *Yakobo 2:5 Mverani abale anga okonedwa kodi Mulungu sanasankha osauka a dziko lapansi akhale olemera mwa chikhulupiriro, ndi olowa nyumba a ufumu adaulonjeza kwa iwo akunkonda Iye.*

**CHIYAMBI**

Anthu ambiri amatha kuweruza anzawo malingana ndi momwe iwo akuwaonera kapena mmene iwo amakhalira. Kodi inu mumaweruzana anzanu potengera chiyani? Ambiri amatha kuyikidwa mmaudindo chifukwa cha maphunziro awo, kukhala achuma, kuchenjera kwawo, kapenanso chifukwa cha kutchuka kwawo ngakhale kuti udindowo sakutha kuyendetsa bwino. Chimodzimodzinso pali anthu ena omwe ali ndi kuthekera kuchita zinthu bwino koma chifukwa iwo ndi osauka kapena osatchuka ndi osaphunzira kweni kweni anthu sawapatsa mwayi woti atsogolere, uku ndiko kusankha kwa dziko lapansi. Palinso a chuma ambiri omwe anapalamula milandu yosiyanasiyana koma chifukwa cha chuma chawo ndi kutchuka kwawo milandu yawo siyipita patali pamene osauka ndi wosatchuka akuthera ku ndende. Phunziro lathu la lero Yakobo akutiuzana kuti Mulungu sasankha monga momwe ife timachitira koma kuti ngakhale wopanda pake Mulungu amawasankha kuti akakhale wolemera mwa chikhulupiriro.

**MAFUNSO**

1. Fotokozani momwe anthu amasalidwira potengera zaka zawo, chuma chawo, mpingo wawo kapenanso ndale.
2. Kambiranani mau oti kukondera mu vesi loyamba ndi mau oti kusankhana mu vesi 9 polumikizana ndi mpingo ndi chikhulupiriro.

3. M'chifukwa chiyani malemba akuchenjeza kwambiri za mchitidwe umenewu , Levitiko 19:15, Masalmo 82:2, Machitidwe 10:34?
4. Kodi Yakobo amathanthauza chiyani ponena kuti Mulungu anasankha osauka a dziko lapansi {vesi 5} Nanga zikufanana bwanji ndi zomwe Yesu analankhula pa Mateyu 5:3.
5. Kambiranani ngati phunziro lathu likutanthaza kuti achuma onse alibe gawo pamaso pa Mulungu.
6. Kodi ndi anthu ati kapena magulu ati a wanthu omwe inu mumasauka nawo ndi kuwaweruza mwa kudziko mosiyana ndi momwe Mulungu amaweruzira?
7. Achinyamata tingapange bwanji kuti tionetse kuti pakati pathu palibe tsankho koma kuti tonse tili chimodzimidzi monga momwe Mulungu amationera

Kusalana kungakhale ndi zotsatira zoipa pa kufalitsa uthenga wabwino monga mboni zotsatira Yesu. Apa mchifukwa chake Yakobo anaona chinthu chofunika kwambiri kuwachenjenjeza atsogoleri kuti asamakondere pomwe akugwira ntchito ya Mulungu. Zingathe kuoneka ngati akuchita ntchito yabwino koma pa kusala anthu ena anali kuchimwira Mulungu. Mulungu anatilenga tonse mchifanizo chake ndipo alinafe cholinga. Inu munayamba mwaganizapo kuti mchifukwa chiyani Mulungu anakulengani ndi kukuikani ku dziko lapansi lino. Alipo lero achinyamata ambiri omwe amasankhana potengera mtundu wawo, mpingo wawo kapenanso komwe amachokera. Koma Mulungu akutilangiza kuti tisamasankhane koma kuti tonse ndife amodzi mwa Yesu ambuye wathu.

Nthawi zonse pomwe achinyamata okhululupirira akupanga ziganizo kapena kuweruza ayenera kupanga zimenezi mogwirizana ndi mfundo za Mulungu kapena tingapezeke tokha tikutsutsana ndi Mulungu wathu. Mzachidziwikire kuti Yakobo amawalembera atsogoleri ake kuti amasalana ndi anthu osauka poona kuti akuchita bwino koma anali kutsutsana ndi Mulungu. Yakobo amafunanso kufotokoza kuti anthu osauka omwe analibe chuma cha dziko lapansi amayika chidwi chawo



kwambiri pa za Mulungu, kusiyana ndi anthu olemera a dziko lapansi omwe nthawi yawo yambiri amasamalira chuma chawo. Yesu adanenanso kuti m'kwapafupi ngamira kulowa pa diso la singano kusiyana ndi munthu wolemera kuti akalowe mu ufumu wa kumwamba. {Mateyu 19:24} Ufumu wa kumwamba walonjezedwa kwa onse amene amamkonda Mulungu ves 5.

Achinyamata tidadziyang'anire pansu ayi chifukwa Mulungu amaona zazikulu mwa ife, anthu angathe kuweruza ndi maphunziro athu, chuma chathu, kutchuka kwathu, kuchenjera kwathu, koma Mulungu amaona mtima wodzipereka ndi wosweka kuti akachititse manyazi zamphavu za dziko lapansi.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu alibe tsankho ndipo akufuna tonse timutumikire ndi kuthekera komwe tili nako lero komanso ku nthawi zonse

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Amosi 5:7-15, Yakobo 1:19-27, Masalmo 68:1-13, Luka 4:16-30, Yakobo 5:1-11, 2:1-12.

**MULUNGU AYITANIRA ANTHU AKE KUKUUNIKA**

**Lemba la phunziro:** 1Petro 2:1-10

**Vesi Loloweza:** *1 Petro 2:9 Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za Iye amene anakuitanani muturuke mundima, mulowe kuunika kwache kodabwitsa.*

**CHIYAMBI**

Gawo lino la maphunziro athu tawonamo kwambiri za kuchoka ku m'dima kupita kukuwala. Anthu amafuna kudziwa kuti miyoyo yawo ikupita kwina kwake, ndi kuti miyoyo yawo ndi yofunika ku dziko lino. Kodi nzotheka kumva ndi kuona kuti moyo wako ndi ofunika? Izi nzotheka ngati miyoyo yawo ikuyenda mkuwala osati mu mdima. Nthawi zonse mdima umapereka chiopsezo ku miyoyo yathu ngakhalenso katundu wathu. Koma mchifukwa chiyani achinyamata ambiri amayendabe mu mdima lero? Komanso si achinyamata okha poti ngakhalenso akulu amene ali mu mdima wadzawoneni ndipo ntchito zawo ziwatsimikizira kuti ali mu mdima. Phunziro lathu la lero pomwe tikumaliza chigawo chino cha kotale wathu Mulungu akuyitanira anthu ake ku kuunika kosatha.

**MAFUNSO**

1. Kodi m'chifukwa chiyani achinyamata amafuna kumva kuti mmoyo wawo muli china chake chofunika? Nanga timachitanji tikadziwa kuti moyo wathu ulibe tanthauzo?
2. Kodi Petro anamufotokoza bwanji Yesu ngati mwala wamoyo vesi 4?
3. Kambiranani momwe Yesu angakhalire mwala wapa Ngodya vesi 4, mwala wokhumudwitsa ndi thanthwe lophunthwitsa vesi 6 mpaka 8.
4. Fotokozani kufunika koti mpingo ukhale ndi Yesu monga mwala wa maziko.

5. Kodi ife achinyamata okhulupirira tikumangidwa bwanji monga nyumba ya uzimu yomangidwa pa maziko akhristu Yesu {vesi 5}
6. Kambiranani njira zomwe mpingo wa chipangano chakale, unsembe ndi nsembe zingatithandizire kumvetsa udindo wathu pa pangano latsopano monga anthu osankhidwa a Mulungu.
7. Fotokozani kuti kodi kukhala anzake akumanga ufumu wa Mulungu zimapereka tanthauzo lotani ku moyo wanu?
8. Kodi inu achinyamata muli ndi mwayi ndi udindo wotani pokhala anthu osankhidwa a Mulungu, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wake Mulungu? Nanga inu ndinu wodzipereka bwanji ku udindo umenewu?

## **KUFOTOKOZA**

Nthawi zambiri anthu safuna kuyenda mu m'dima ndipo amasankha ngakhale kuyenda ndi chowunikira mmanja mwawo. Koma chokhumudwitsa mchakuti pomwe anthu akuyenda mu mdima mmoyo wawo wa uzimu alibe nazo nkhwawa bola moyo wawo watsiku ndi tsiku ukuyenda. Moyo wathu wa uzimu wayenera kukhala ndi komwe tikupita {destination} ndipo tayenera kuyenda ndi cholinga. Pomwe moyo wathu ukuyenda mu mdima zimadetsa nkhwawa za tsogolo lathu.

Petro analemba kalatayi pofuna kuti achinyamamta ndi anthu onse omwe atembenuka mtima ayende mmoyo osiyana ndi omwe anauzolowera, koma kuti asiye zonse zoipa ndi ntchito za mundima, zachinyengo ndi zachabe. Izi zikukhudza moyo wathu walero kuti pomwe tatembenuka mtima tayenera kusonyeza moyo wa Khristu Yesu mkati mwathu. Achinyamatanso kuyenera kudziwa ndi kuzindikira kufunika kwa moyo wathu pamaso pa Mulungu ndi kumugwilira ntchito yake mmagawo onse a moyo wathu.

Kukula ndilo gawo lina lofunika zedi mmoyo wa chikristu kuphatikizapo kuyenda ndi Iye. Mkutheka Petro amalemba anthu omwe anangotembenuka kumene kapenanso kuti anthuwo ntchito zawo zinali

zamumdima zokha zokha. Ndizofunika kwambiri kumakumbukira kuti ndife yani ndipo tayenera kuchita chiyani. Izi zingatithandize ife kuti tisataye chidwi chathu pa Yesu Khristu ndi mayitanidwe athu popeza ife tayitanidwa kukayenda mkuwala ndi kusiyana nawo mdima. Mwa ichi Petro akukukumbutsani inu achinyamata kuti ndinu mtundu wosankhidwa, ansembe achifumu, mtundu woyera, komanso anthu a mwini wake. Vesi 9. Talandira ulemu onsewu koma tizindikirensa kuti talandira ulemuwu kuti tikalalikire za mphamvu zake za Iye yemwe watiyitana tichoke mu mdima ndi kulowa mkuunika kwake kodabwitsa. Kuyenda kwathu mkuunika kwayeneranso kukhala ndi udindo wake. Yesu ndiye kuwala kwa dziko lapansi ndipo onse woyenda ndi Iye sadzakhala mu mdima nthawi zonse.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Yesu Khristu ndiye kuunika kwenikweni ndipo woyenda ndi iye sadzakhala mu mdima nthawi zonse.

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

1 Atesalonika 5:1-10, Akolose 1:9-22, 1Timoteo 6:11-16, Yesaya 42:8-17, Masalmo 119:121-136, 1Petro 2:1-25

**KUPEREKA CHIYEMBEKEZO KU NTHAWI YA M'TSOGOLO**

**Lemba la phunziro:** Yesaya 29:13-24

**Vesi Loloweza:** *Yesaya 29:24 Iwo osochera mumzimu adzadziwa luntha, ndi iwo amene ang'ung'uza adzaphunzitsidwa.*

**CHIYAMBI**

Maubwenzi amasweka chifukwa chakusakhulupirika kwa anthu. Kodi inu munayamba mwakhalapo osakhulupirika pa ubwenzi wanu kapena munaonapo wina atatero? Yesaya analosera kuti Yehova adzalanga anthu ake koma sadzaleka kuwachitila chifundo ndipo adzawabwenzeletsa kudziko la lonjezano patapita nthawi.

**MAFUNSO**

1. Kodi mumalandira bwanji chidzudzulo?
2. Kodi mu Yesaya 29:1-12 akufotokoza zotani? Ndi chilango chotani chomwe chimayembekezedwa
3. Nanga chimadza pa zifukwa ziti?
4. Fotokozani zomwe Mulungu anadana nazo mu vesi 13 ya Yesaya. Nanga Yesu anagwiritsa ntchito bwanji mau a mu vesi 13 ku Mateyu 15?
5. Ndi machenjezo otani omwe tingatenge mu mauwa?

**KUFOTOKOZA**

Phindu la kusamvera sitimakondwera ndi kudzudzulidwa, tikamva mau otsutsa ganizo lathu. Mavuto akudza chifukwa cha kusamvera zimavuta kwambiri kulandira izi, tikakhumudwitsa yemwe timamukonda timamva kuwawa koposa kulandira chilango pa nkhaniyi. Ndizosavuta kuchita tchimo kapena maganizo apa koma zimavuta tikamalandira chilango chake. Aneneri a m'chipangano chakale amatumidwa nthawi ndi nthawi

ndi Yehova Mulungu kukapereka uthenga wodzudzula komanso chilango chomwe adzalandire chifukwa cha tchimolo. Iwo amalimbikitsa anthu kulapa kuti Yehova aleke kuwalanga. Yesaya ndi m' modzi mwa aneneri oterewa, werengani maitanidwe ake mu Yesaya.

Mu Yesaya 26 mpaka 31 tikumvamo uthenga waukulu odzudzula Yuda. Mu Yesaya 28:8 “pakuti magome onse adzadzadzidwa ndi masanzi ndi udio, palibe malo okonzeka”

Ngakhale anthu amalemekeza miyambo yopembedzera Yehova chaka ndi chaka mitima yawo simalunjika ku zomwe amangochita mwa chizolowezi. Yesaya ananenera kuti Yerusalemu adzathiridwa nkhondo ndipo adzatsitsidwa. Yehova kudzera mwa Yesaya komanso kutenthedwa kwa linga la Yerusalemu.

Mu vesi 13 Yehova akufotokoza kuti anthu ake amangolemekeza ndi mkamwa mwawo koma mitima iri kutali. Yesu Khristu akugwiritsa ntchito mawuwo kuphunzitsa anthu kuti choturuka mkamwa chimaipitsa munthu. Izi ndi zolankhula komanso ntchito za munthuyo. Akhungu akamatsogolera njira amagwa m' mbuna werengani Mateyu 15 zoturuka zoturuka mkamwa zimachokera muntima ndipo kudzera mwa aneneri kuti ngati Yuda atalapa adzamuchitira chifukwa komanso chilangochi chidzatha ndipo Yuda adzabweleranso kwao ngakhale chilango chidzakhale chachikulu ndi chowawa. Choncho pamene mu kotale uyu pamene tikuona za kuturuka mundima tiyeni malingaliro ndi zochita zathu zikhale zolemekeza ndikupereka ulemu woyenera pamaso pa mfumu Atate wathu.

## **PHUNZIRO**

Tiyenera timve chidzudzulo ndipo tizidziwa kuti chilango ndi chowawa.

## **MALEMBA OWERENGA KUNYUMBA**

1 Akorinto 5:1-5, Eksodo 23:1-9, Yeremiya 29:10-14, Marko 7:1-8, Yesaya 29:1-8, Yesaya 29:9-12.

# **CHIGAWO CHA CHIWIRI**

## **MULUNGU AKHALA PAKATI PA ANTHU AKE**

### **PHUNZIRO 1**

**7<sup>th</sup> October, 2023**

### **MULUNGU PAKATI PATHU**

**Lemba la phunziro:** Chibvumbulutso 21:9-10, 22-27. 22:1-5.

**Vesi Loloweza:** *Chibvumbulutso 22:5 Ambuye Mulungu adzawaunikira ndipo adzachita ufumu ku nthawi za nthawi.*

### **CHIYAMBI**

Anthu amamva bwino kuzindikira kuti pakati pawo pali munthu wina wamkulu. Izi zimapangitsa anthuwo kukhala womasuka ndi kumva kuti ali wotetezeka. Pamene Yesu wapita kukatikonzera malo akupanga zinthu ziwiri, zomwe ndidziko latsopano ndi m'mwamba mwatsopano.

Mukayang'ana dziko lino muona kuti kuli pansi pomwe timayendapo ndi m'mwamba mwake. Dziko lomwe Yesu akukonzera anthu ake lidzakhala chimodzimodzi ndipo kudzakhala m'mwamba ndi pansi pake ndipo zonse zatsopano sikudzakhala Nyanja. Chachiwiri chomwe akupanga ndicho mzinda wa Yerusalemu watsopano umene udzatsika. Sikudzakhala kachisi popeza kachisi adzakhala Mulungu mwini, sikudzakhalanso mwezi, dzuwa ndi nyenyezi popeza Yesu Khristu mwini adzakhala nyali ya mzindawo. Ndipo tidzakhala wosangalala nthawi zonse ndi Mulungu pakati pathu ndi Yesu ali nyali ndi mfumu yathu.

### **MAFUNSO**

1. Kodi m'modzi wa angelo asanu ndi awiri adanena chiyani kwa Yohane? nanga anamuonetsa chiyani
2. Kambiranani chifukwa chiyani mu mzindawo simudzakhala kachisi komanso dzuwa, nyenyezi ndi mwezi.
3. Fotokozani komwe kudzakhale mzindawo ndipo anthu omwe adzakhale mu mzindawo ndi ndani?

4. Mu vesi 24 akukamba za amitundu. Kodi amitundu amenewa ndi ndani?
5. Kambiranani ndi ndani adzaone nkhope ya Mulungu mu mzindawo, nanga inunso mudzawona nawo Mulungu [fotokozani]
6. Inu mukuganiza kuti anthu okhala mu mzinda adzachita chiyani nthawi zonse za moyo wawo?
7. Taperekani malangizo ndi uphungu kwa anzanu omwe akufuna kukakhala ku mzindawo.

## **KUFOTOKOZA**

Mundime yathu ya lero tikuonamo za mzinda watsopano wa ukulu ndi wabwino wokonzedwera anthu onse kuyambira mibadwo yomwe inapita, yomwe ilipoyi, komanso yomwe ilim'kubwera. Koma kanthu kosapatulidwa sikakapezeka mu mzinda umenewu. Mwanjira ina ku mzinda umenewu kulibe mdima ndipo onse okonda ntchito za mdima sakapezeka ku mzinda umenewu. Izi zikungofuna kutikumbutsa mutu wathu wa kotale uno kuti kuchoka mu mdima ndi kulowa mu kuwala choncho onse omwe adzapezeke kuti ali mu mdima sakalowa nawo mu mzinda umenewu. Sikudzakala kachisi chifukwa Ambuye Mulungu wathu ndiye kachisi wake komanso matupi athu ndiwo adzakhala kachisi wopatulika wa Mulungu wathu 1 Akorinto 6:16

Pamene Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi zonse zinali zabwino ndithu koma zinaonongedwa ndi uchimo, munthu atachimwa pamaso pa Mulungu. Kumbukirani chigumula cha Nowa pamene dziko linamizidwa ndi madzi ndipo zinthu zonse zinaonongedwa. Kuyambira nthawi imeneyo dziko simunakhalenso mtendere ayi koma mavuto okha okha koma tsopano Mulungu akulonjeza kukhala ndi anthu ake mu mzinda watsopano wopanda mavuto ndi masautso. Iyi ingakhale nkhani yokondweretsa pakati pa achinyamata ambiri omwe atopa ndi ulova, matenda, imfa, maudani, njala, nkondo, umphawi, ndi zina zambiri.



## **PHUNZIRO KWA IFE**

Achinyamata tichite changu kuchoka mu mdima ndi kulowa mkuunika kuti tikakhale ndi Mulungu wathu ku nthawi zonse.

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Aroma 3:1-10, 1 Akorinto 1:1-9, 10:1-13, Yesaya 44:1-10, Masalmo 56:1-10.

**THAWA CHOYIPA**

**LEMBA LA PHUNZIRO:** Miyambo 6:16-28

**Vesi Loloweza:** *Miyambo 6:20 Mwananga sunga malangizo atate wako, usasiye malamulo a amako.*

**CHIYAMBI**

Pamene tikupitiliza ndi kuona mau oti kuchoka mu mdima ndi kulowa mu kuwala kodabwitsa komwe Mulungu wakonzera anthu ake lero tionanso mau oti thawa choipa. Mau oti **“Thawani”** ndi mau ochenjeza komanso mau oopseza. Nthawi zambiri sitiyanba tafunsa tikamva mau otere koma kuyamba kuthawa. Wolembe sakufuna kuti tingopewa chabe zoipa kapena kuti pomwe tikuchoka mundima tichoke mwa mtambasale ayi koma tithawe ndithu. Akupereka chithunzi cha dama, ndi chiwerewere poyerekeza ndi chikoka choipa chomwe dama ndi chiwerewere chimakhala nacho pokopa achinyamata kukhalabe mu mdima. Tchimo ukamaliyandikira limatha kukopa mosayembekezera ngakhale kuti sichinali cholinga chako kuchita tchimolo. Achinyamata ambiri anakopeka m’njira monga imeneyi ndipo lero adagwa m’zosautsa. Ena analephera kumaliza maphunziro awo, ena business zawo zidasokonekera komanso mwina kuchita misala kumene. M’chifukwa chake phunziro lathu la lero akutiiza kuti thawa choipa.

**MAFUNSO**

1. Fotokozani zinthu ziwiri zomwe Mulungu azida ndipo kambiranani m’chifukwa chiyani Mulungu azida zinthuzo.
2. Kambiranani kuti kodi zinthu zimenezi zimatanthauza chiyani chilichonse pachokha pachokha.
3. Kodi malamulo omwe ali mu ndimeyi akuchokera kwa ndani ndipo akupita kwa ndani?

4. Kambiranani za kufunika komvera malamulo a Mulungu komanso akulu pa moyo wathu monga achinyamata.
5. Fotokozani za machenjezo omwe ndimeyi ikutsiliza nawo.
6. Mukuganiza kuti zotsatira za kusamvera machenjezo amenewa zingakhale zotani pa moyo wa achinyamata a lero?
7. Kambiranani komwe ife achinyamata tingathawire pomwe tikuthawa tchimo ndi kusunga malamulo

## **KUFOTOKOZA**

Ndimeyi muli zinthu zisanu ndi chimodzi zimene Mulungu azida, ndi zinthu zisanu ndi ziwiri zimene Mulungu zim'nyasa. Mulungu akusaka achinyamata amene amapembedza Mulunguyo ndi mtima wawo onse komanso amene akuchita zoyenenera pamaso pake. Mulungu amakonda anthu amene amalankhula zoono, odzisunga, amaganizo abwino, ofunitsitsa kuchita zabwino, achilungamo ndi mtendere.

Paulo anamuchenjeza mwana wake mu uzimu Timoteo kuti athawe chikondi cha dziko lapansi ndipo afunefune chilungamo, chipembedzo, chikhulupiriro ndi chikondi. [1Timoteo 6:11] Paulo adadziwa kuti ngati Timoteo angakhalebe mu zinthu zimenezi adzatayika ndi kuonongeka ndi dziko lapansi.

Malamulo a Mulungu ali nyali ya kumapazi athu ndi kuunika kwa pa njira yathu choncho munthu asadzatinamize kuti malamulo adatha, ayi dzadziweni kuti iye akuyendabe mu mdima ndipo choonadi cha Mulungu sichikhala mwa iye. Wosunga lamulo asunga moyo wake koma wonyalanyaza mayendedwe ake adzafa.

## **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu akufuna ife achinyamata tiyende m'chiyero moyo wathu onse ndi kupulumutsidwa ku m'badwo uno.

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Aroma 7:1-19, 1 Timoteo 6:1-10, Luka 6:22-45.

**KWATHU KWATSOPANO****Lemba la phunziro:** Chibvumbulutso 21:1-8

**Vesi Loloweza:** *Chibvumbulutso 21:1 Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano, pakuti m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka, ndipo kulibenso Nyanja.*

**CHIYAMBI**

Achinyamata maka ana amakondwa kudziwa kuti alinso ndi kwawo kwina koposa kumene akhalako tsopano. Inu mumamva bwanji kuzindikira kuti mulinso ndi kwanu kwina koposa ku dziko lino? Ana a Israeli atakhala ku dziko la Aigupto kwa zaka zochuluka anayamba kumva mbiri kuti alinso ndi kwawo kwina komwe makolo awo amkakhala komanso komwe Mulungu wa makolo awo anawalonjeza kuti adzakhalako ku nthawi zonse. Nthawi zonse akamakhala anayamba kulingalira zobwerera kwawo kusiyana nalo dziko la Aigupto. Atauzidwa kuti ulendo uja wayandikira ndipo aliyense atenge mwana wa nkhosa aphe, magazi ake apake pa mphutho za nyumba zawo izi adachita motero popeza mitima yawo inalingalira zopita kwawo kuchoka m'dziko la chilendo. Yesu atatha kutipulumutsa anaona kuti ndikofunika kuti apite kwa atate ake akatikonzere malo, Yohane 14:1-6. Atatha kukonza dzikolo adzabweranso kudzatitenga kuti ifenso tikakhale ku dziko latsopanolo komwe sikudzakhala madzi kapena Nyanja, Chibvumbulutso 21:1. Phunziro lathu la lero likutitengera kwathu kwatsopano kuposa komwe tili kukhala lero lino.

**MAFUNSO**

1. Inu mumamva bwanji kuti muli ndi kwanu kwina koposa kuno komwe mukhalako, nanga anzanu mungawauze zotani za izi?

- 2 Kodi chidzachitika ndi chiyani ndi m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba lija?
- 3 Tafotokozani bwino za maonekedwe a dziko latsopano ndi m'mwamba mwatsopano momwe Khristu Yesu Ambuye watikonzera
- 4 Kambiranani za mau oti “**Taona chihema cha Mulungu chili mwa anthu ndipo adzakhalitsa nawo**“ akutanthauza chiyani?
- 5 Kambirani kusiyana kwa m'mene Mulungu akukhalira nafe lero ndi m'mene adzakhalire nafe mu mzinda wa Yerusalemu watsopano?
- 6 Wolemba buku la Chibvumbulutso akuti sikudzakhalanso Nyanja komanso sikudzakhalanso imfa. Kodi izi zikutanthauza chiyani za mzinda watsopanowu?
- 7 Inu mukuona kuti m'chifukwa chiyani sipadzakhalanso imfa mu mzindawu? Fotokozani mau oti “*kulakika*” akutanthauza chiyani, Nanga Mulungu akulonjeza chiyani kwa iwo wolakika.

## **KUFOTOKOZA**

Yohane anaona mzinda watsopano woyerawo uli m'kutsika kuchokera kumwamba kwa Mulungu, wokonzedwa ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wake. Ndipo anamva mau akuti, “***Taona chihema cha Mulungu chili mwa anthu ndipo adzakhalitsa nawo***“ Pamene Mulungu akukhala ndi okhulupirira lero mu mzimu, adzakhala nawonso mu Yerusalemu watsopano kumene sikudzakhala tchimo, koma adzakhala m'chiyanjano ndi Mulungu. Mulungu adzapereka madzi a moyo kwa ulele kwa iye wakumva ludzu [Yesaya 55:1, Yohane 4:10, Aroma 3:24, Chibvumbulutso 21:6 ] Uwu ndi moyo wa uzimu ndi wosatha kumwamba. Kodi ife tidzakhalako?

Yohane akupereka chithunzi-thunzi cha mzinda watsopano kuti ife achinyamata amene timakonda dziko lapansi ndi ntchito zake tikhalenso ndi chidziwitso cha zomwe Mulungu wakonzera anthu ake. Pali anthu ambiri omwe sakhulupirira kuti kuno sikwathu ndipo tayenera kuti tsiku lina tidzabwerere kwathu. Anthu otere amakhala ku dziko lino mwa

mtambasale ndi mopanda nkhawa ndipo ambiri a iwo safuna ngakhale kuuzidwa kuti tsiku lina kuno adzachoka maka polingalira zomwe dziko lapansi limawapatsa. Achinyamata tisanyengeke ndi chuma chathu, maphunziro athu, kutchuka kwathu, udindo wathu popeza zonsezi zidzatsala ndipo sizidzakhoza kutiyimira pa mlandu wathu koma Yesu yekha basi.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Chikhale chokondweretsa kuzindikira kuti tili ndi kwathu kwina komwe Ambuye atikonzera malo koposa kuno ndipo tikachita bwino tikalowako ndi kukhala komko ku nthawi za muyaya.

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

2 Petro 3:8-14, Yesaya 65:17-25, Chibvumbulutso 25:1-10, Ezekiel 36:22-30, Chibvumbulutso 21:9-27

**KHRISTU NDI MFUMU YATHU**

**Lemba la phunziro:** Luka 19:28-40

**Vesi Loloweza:** *Luka 19:38 Wolemekezeka mfumuyo ikudza m'dzina la Ambuye, mtendere m'mwamba ndi ulemelero m'mwamba-mwamba.*

**CHIYAMBI**

Phunziro lathu la sabata yatha tinazindikira kuti tili nako kwathu kwina koposa kuno komwe tikhalako. Kumeneko kulibe kachisi chifukwa Mulungu wathu ndiye kachisi. Kulibenso dzuwa, mwezi ndi nyenyezi chifukwa Khristu Yesu ndiye kuwala kwathu kodabwitsa. Chosangalatsa china m'chakuti kulibenso maliro, matenda, umphawi, njala, ngakhalenso udani popeza tonse tidzakhala ndi mtima umodzi kutamanda Yohova Mulungu wathu. Phunziro la lero tionanso za mfumu ya mzinda watsopano umenewu.

M'malo mwa Mulungu, Yesu Khristu anatipatsa ife ufumu wa Mulungu ndi a nsembe ake, komanso monga Yesu ali mwana wa Davide ku thupi ali mfumu ya Israeli. Onse omwe anamulandira Khristu Yesu Ambuye ali pansu pa ulamuliro wa Yesu nasiyana nazo ntchito za mu mdima ndipo Yesu akhala mfumu yawo. Machitidwe 1:6, Yesu adzafika monga mfumu yathu pa dziko lapansi asanatenge anthu ake kupita nawo kumwamba kumene akukonza. Iye adzakhala mfumu kufikira atayika adani ake pansu pa mapazi ake. [Chibvumbulutso 20:7-10, 1 Akorinto 15:24-26] Choncho Yesu akukhala mfumu yathu mu mzinda wathu watsopano.

**MAFUNSO**

1. Kambiranani zomwe Yesu anauza ophunzira ake kuti akachite mu mzindawo

2. Fotokozano zomwe zinachitika nthawi yomwe ophunzirawo amamasula bulu uja, ndipo mukuganiza kuti m'chifukwa chiyani mwini wake wa bulu uja sanakanize?
3. M'chifukwa chiyani Yesu anatuma ophunzira ake kuti akamasule bulu uja
4. Kambiranani zomwe zinachitika Yesu atakwera pa bulu uja ndipo zimenezi zimatanthauza chiyani?
5. Inu mukuganiza kuti m'chifukwa chiyani Afarisi ndi Alembi sadakondwere ndi zochitikazo pamene anthu ena adali kuonetsa chimwemwe chawo?
6. Kambiranani ngati pa mpingo pathu pali anthu a mtima ndi maganizo ngati a Afarisi ndi Alembi, nanga tingawathandize bwanji?
7. Mungasiyanitse bwanji ufumu womwe Yesu akubwera kudzakhazikitsa ndi ufumu wa dziko lapansi lero
8. Achinyamata fotokozani za chimwemwe chanu podziwa kuti Yesu ndiye mfumu yathu ndipo tidzakhala ndi Iye ku nthawi zonse.

## **KUFOTOKOZA**

Kumvera ndilo gawo limodzi lofunika kwambiri pa moyo wachikhristu. Baibulo limatiuza kuti kumvera kuposa nsembe zopsereza. Ife achinyamata tayenera kuphunzira kumvera ndi kutsatira malamulo ngakhale tisaone zotsatira zake popeza ichi ndicho chikhulupiriro. Ophunzira ake a Yesu anauzidwa kukatenga bulu ngakhale anali asanamuone komanso mwini wake wa buluyo samamudziwa koma anangochita zomwe analamulidwa kuchita ndi Ambuye wathu Yesu. Yesu akulamulira kuchita chimodzi-modzi.

Yesu atakwera pa bulu anthu anayala zovala zawo mu mseu, ena anatenga kanjedza ndikuyala mu msewu nyimbo zawo zili pakamwa hosanna, hosanna hosanna mfumu yathu. Anthu sanangobwera pamaso pa mfumu yawo opanda kanthu m'chifukwa chake aliyense amayala chomwe anali



nacho moyamika mfumu yawo. Ifenso tayenera kupereka zomwe tili nazo pamaso pa mfumu yathu Khristu Yesu mokondwera.

Kumulemekeza monga mfumu ya mafumu ndi mbuye wa ambuye kuyambira m'maganizo ndi mu ntchito. Yesu analowa mu Yerusalemu ndi anthu ambiri, ndipo iwo adamulemekeza ndi kumuyimbira chifukwa cha ntchito zazikulu adawachitira. Yesu Khristu ali mfumu ya dziko lonse ndipo ngakhale amene adavomereza kuti Khristu ndi Ambuye iye akhala mfumu yawo lero.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Tidze kwa Yesu monga mfumu yathu ndi ulemu woyenera. Ntchito zathu zionetse ulemu kwa Ambuye wathu, ndipo tituluke mu mdima wa uchimo kuti tikakhale ndi iye ku nthawi zonse.

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

1 Timoteyo 1:1-17, 6:1-15, Luka 10:10-24, 1 Petro 1:10-17, Mateyu 22:1-5.

**YESU ATIPEMBEDZERA IFE**

**Lemba la phunziro:** Ahebri 4:14, 5:1-10

**Vesi Loloweza:** *Ahebri 4:15 Pakuti tili naye wansembe wosatha kumva chifundo ndi zofooka zathu koma wayesedwa mzonde monga momwe ife koma opanda uchimo.*

**CHIYAMBI**

Nthawi zina anthu ena amagwira ntchito m'malo mwa anthu ena omwe sangathe kugwira ntchitoyo, kapenanso kuti ntchitoyo sangagwire bwino mwa iwo okha. Kudziko kunonso kuli anthu ena omwe amayimira anzawo pa milandu yawo [Lawyers] ndipo amayesetsa kuti anthu omwe akuwayimirawo nkhani iwakomere ndipo asamangidwe. Awa ndi anthu adziko lapansi omwe nthawi zina zinthu zimawavuta ndipo woyimilidwayo amatha kumangidwa ndithu.

Wolembe bukhu la Ahebri akutiuzwa ife kuti Mulungu anasankha Yesu mkulu wansembe kukhala wopembedzera m'malo mwa anthu a Mulungu. Pamene tili ku dziko lino ngakhalenso dziko latsopano sitingathe ife kuchita bwino mwa ife tokha popeza tili anthu ofooka ndipo Mulungu anatichepsa pang'ono natilekanitsa ndi angelo mwa ichi panasoweka wina wotithandizira ndiye Khristu Yesu.

**MAFUNSO**

1. Kambiranani zomwe inu mumadziwa za wansembe wamkulu
2. Fotokozani ntchito ya wansembe ndi yotani? Nanga wansembe ndi wofunika bwanji?
3. Kambiranani ngati mkofunika kwa achinyamata kukhala ndi wansembe wotiyimira pamaso pa Mulungu.
4. Yesu monga wa nsembe mungamusiyantse bwanji ndi ansembe omwe akupezeka m'mipingo ina lero lino?

5. Fotokozani zinthu ziwiri zomwe zafotokozedwa mu Ahebri 4:14-15 zomwe Yesu analinazo ndipo zinamuyenereza bwanji Yesu kukhala mkulu wansembe kolingana ndi Ahebri 5:7-10
6. Mazunzo a Yesu akuonjezera bwanji mphamvu kukhala wansembe wamkulu wathu nanga mkofunika bwanji kuti Yesu adzitipembedzera mmalo mwathu?

## **KUFOTOKOZA**

Vesi lathu lotsegulira Ahebri 4:14, likubwereza mutu 3:1 ndi kusindikiza kuti Yesu ndi mkulu wansembe ndi woyenera ku m'kweza molimbikitsa chikhulupiriro. Nkhani yabwino imene wolembe akufotokoza ndi yoti ngakhale Yesu anayesedwa m'njira ina iliyonse koma sanachimwe. Tikulimbikitsidwa kuti maganizo a Yesu pa anthu ochimwa ndi kumva nawo chisoni. Yesu Khristu anamvetsa kufooka kwathu ndipo kuchokera m'chifundo ndi m'chikondi anazipereka yekha kukhala nsembe ya machimo athu. Anakhala omvera m'malo mwa ife ndi kulandira chilango chathu kuti ife tikhale ndi moyo. Mwa ichi iye apitilizabe kutipembedzera kuti ife tikhale ndi moyo.

Pa Aroma 3:23 akuti pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemerero wa Mulungu, ndikofunika kwambiri kwa ife kugwira chikhulupiriro chimenechi ndi kukhululupirira kuti Yesu ndi njira yokhayo ya chipulumutso, chifukwa Iyeyu anazipereka yekha nsembe chifukwa cha zochimwa zathu ndipo akupitiliza kutipembedzera pamaso pa Mulungu atate wake.

## **PHUNZIRO KWA IFE**

Ife achinyamata tione momwe Yesu anakwaniritsira ntchito yotipulumutsira ndi kukhala mkulu wa nsembe

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Yakobo 5:1-18



**KUPEMPHERERANA WINA NDI M'NZAKE****Lemba la phunziro:** Yakobo 5:13-18

**Vesi Loloweza:** *Yakobo 5:16 Chifukwa chake muvomerezane wina ndi m'nzake machimo anu ndipo mupemphelerane wina ndi m'nzake kuti muchiritsidwe, pemphero la munthu wokhulupirira likhonza kwakukulu m'machitidwe ake.*

**CHIYAMBI**

Nthawi zambiri pomwe tikukhala ndi wokondedwa athu timafuna kukhala nawo nthawi zonse, ndipo ngati wina achoka kudzera mu imfa timakhala wokhumudwa chifukwa sichomwe chimakhala chiyembekezo chathu. Komanso pali abwenzi athu omwe sadatembuke mtima ndipo iwo achitabe ntchito za mu mdima ife timamva bwanji za iwo? Lero mu phunziro lathu tikambirana za kupemphererana wina ndi m'nzake.

Moyo wathu umadutsa mu nyengo zosiyanasiyana ndipo ife tayenera kudziwa nyengo zathu ndikuchita choyenera. Kudwala ndi mbali imodzi ya moyo wathu ndipo tikadwala timakhumudwa ndi kusowa mtendere. Yakobo polemba bukhu lake akubweretsa pamodzi umodzi wa chikhristu popemphererana wina ndi m'nzake maka pomwe wina wadwala komanso ali m'mavuto wosiyana-siyana. Pemphero sikungoyankhula monga momwe ena achiyesera ayi koma kuyankhula ndi Mulungu mwa chikhulupiriro. Ndipo pomwe abwezi athu adwala tayenera kupemphera ndi chikhulupiriro ndipo iwo adzachira ndithu, tisayiwale kuti tikuchoka mu mdima ndi kulowa mkuwala kodabwitsa kwa Mulungu wathu. Mulungu walonjeza m'mwamba mwa tsopano ndi dziko latsopano ndipo tayenera tonse kukafikako ndipo tayenera kupemphererana wina ndi m'nzake kuti tikakhalire limodzi kwa nthawi zosatha.

**MAFUNSO**

1. Mu vesi 13 fotokozani ndi ndani akuyenera kupemphera ndi kuyimba?

2. Kambiranani nthawi ndi nyengo zomwe munthu wayenera kupemphera ndi kuyimbira malingana ndi Yakobo.
3. Fotokozani pali mgwirizano wanji pakati pa **kukhululukirana** wina ndi m'nzake ndi **kupempherana**.
4. Fotokozani zomwe tikuphunzirapo mu ndime yathu ya lero za kukhululukira ndi kupemphera.
5. Kambiranani kuti pemphero la munthu wolungama limachita motani?
6. Kodi mau woti” *kudzonza* ‘akutanthauza chiyani m’ndimeyi?

## **KUFOTOKOZA**

Bukhu la Yakobo linalembedwa kwa anthu amene amadutsa m'mavuto osiyanasiyana. Kuyambira pa chiyambi cha bukhu la Yakobo akutsogolera maganizo athu ku phindu la chipiriro ndi mayesero kuphatikizapo chikhulupiriro ndi kupirira [Yakobo 1:2-4] Potsiliza pa bukhu la Yakobo akubwerera kukumbutsa ife achinyamata kupirira kumene Yobu anali nako pamaso pa zovuta zimene anali nazo. Yakobo 5:10-11.

Yakobo sikuti amalimbikitsa kupirira kokha komanso amatsindika kufunika kwa mphamvu ya pemphero, ngati gulu kapena payekha payekha. Lonjezo limene Yakobo akupereka m'ndimeyi likhale chilimbikitso kwa ife ndi wokonedwa athu kuti Mulungu sadatiyiwale koma akufuna ife tisakhale chete koma tidzimukumbukira nthawi zonse m'mavuto ngakhale pachisangalalo.

## **PHUNZIRO KWA IFE**

Pemphero ndicho chida chathu chogonjetsera mdani wathu ndiye tipemphererane wina ndi m'nzake kuti ife ndi abwenzi athu tichiritsidwe ku nthenda zathu ndi kukalowa mu mzinda watsopano.

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Daniel 1:5-17, Mateyu 6:1-18.

**KUPEREKA MOLOWA MANJA**

**Lemba Laphunziro: 2 Akorinto 9:3-15**

**Vesi Loloweza:** *2 Akorinto 9:6 Koma nditi ichi kuti Iye wakufesa mouma manja, mouma manjanso adzatuta, ndipo iye wakufesa molowa manja, molowa manjanso adzatuta.*

**CHIYAMBI**

Kupereka ndicho chivomerezo chathu kuti Yesu Khristu ndiye mbuye ndi Mpulumutsi wathu. Ichi ndi chifukwa chake Paulo anawauza akhristu a ku Akorinto kuti kupereka ndi umboni wawo [2 Akorinto 9:12-13. Iye anati utumiki wa kupereka suthandiza ntchito za kulalikira uthenga zokha ayi komanso kusonyeza kuthokoza kwathu kwa Mulungu chifukwa cha chipulumutso chimene anatichitira kupyolera m’manzunzo ndi imfa ya Yesu Khristu Ambuye wathu. Ndiye pamene wachinyamata apereka mouma manja amanyazitsa chikondi cha Mulungu kwa iye ndipo Mulungu amam’mana madalitso ake chifukwa cha kusayamika kwake.

Koma pamene m’khristu apereka molowa manja, amayamikira chikondi cha Mulungu kwa iye kusonyeza kuti akukhulupirira kuti Ambuye wampulumutsa ndipo Mulungu amakondwera naye ndi kumtsanulira madalitso wochulukira. Ichi ndi chifukwa chimene Paulo akuti kupereka ndi umboni wathu kwa Mulungu.

**MAFUNSO**

1. Fotokozani bwino zomwe zimachitika kwa ofesa mouma manja ndi wofesa molowa manja.
2. Kodi mau oti [**kufesa mouma manja ndi kufesa molowa manja**] akutanthauza chiyani kwa inu?

3. Kambirani ndondomeko zomwe tingatsate kuti tionetse zoti tatuta molowa manja.
4. Fotokozani za maperekedwe athu poganizira za ndalama, nthawi yathu, komanso zochita zathu pamaso pa Mulungu.
5. Inu mukuganiza kuti Mulungu amamva bwanji ndi kupereka kwathu?
6. Kambiranani za zinthu zomwe tayenera kupereka pamaso pa Mulungu ndipo tayenera kupereka nthawi yanji?
7. Fotokozani za cholinga cha Mulungu potipatsa zinthu zomwe tilinazo.
8. Kodi ndime yomwe tawerengayi ikukuphunzitsani chiyani pa za kupereka mouma manja ndi kupereka molowa manja?

## **KUFOTOKOZA**

Paulo akuwatsimikizira akhristu aku Akorinto kuti kupereka ndi m'dalitso. Kukula kwathu mu chikhristu kumakhudzana kwambiri ndi kufesa kwathu. Pamene wachinyamata akupereka molowa manja zimapekanso mulingo wa kukula kwake mu moyo wa uzimu. Tisayiwale kuti kusakula ndi ulumali ndithu ndipo alipo achinyamata ambiri womwe safuna kukhala ndi ulumali koma ali wolumala mu uzimu ndipo izi zimaonekera ndi momwe iwo akuchitira ndi zopereka zawo.

Chachiwiri Paulo akutionetsa maperekedwe onse awiri ndi zotsatira zake ndizo; kupereka mouma manja, mouma manjanso kututa ndi kupereka molowa manja ndi molowa manjanso kututa. Ndipo akuti ndi kupereka molowa manja timatutanso m'dalitso ndipo sitingalakwitse kunena kuti kupereka mouma manja timatuta temberero. Kututa kwathu kudzakhala kwabwino ngati tipereka molowa manja komanso kuchokera pansu pa mtima. Wopereka molowa manja amalandiranso zambiri kuti athenso kupereka zambiri. Mulungu amapereka zosowa zathu kuti tithe kuchitira umboni wa zochita zathu. Mulungu amafuna wokhulupirira adzipereka mokondwera osati mokakamizidwa kapenanso mwa chisoni, ndipo pakutero amatidalitsa koposa.



## **PHUNZIRO KWA IFE**

Tayenera kupereka pomubwezera Mulungu zabwino zomwe iye amatichitira ndipo wopereka molowa manja, molowa manjanso amamudalitsa.

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Masalmo 24: 1-5, 37:16-24, Yakobo 1:12 -17, Aroma 15:25-29, Luka 6:32-38

**MULUNGU WA CHILUNGAMO**

**Lemba la phunziro:** Masalmo 82:1-8, 113:5-9

**Vesi Loloweza:** Masalmo 82:8. Ukani Mulungu weruzani dziko lapansi pakuti inu mudzalandira a mitundu yonse.

**CHIYAMBI**

Mau akuti Chilungamo si mau achilendo pakati pa achinyamata ambiri lero. Anthu ambiri akufuna chilungamo kudziko lapansi lero ndiye mkumati chilungamocho chikupezeka? Ambiri mwa ana a masiye ndi amai a masiye akuvutika kuti apeze chilungamo. Komanso kuli anthu osauka ndi aumphawi sakupeza chilungamo muzinthu zambiri amangoponderzedwa osapeza chilungamo. Ambiri mwa anthu osauka amafera kundende milandu yawo wosaweruzidwa kapena kuweruzidwa mokondera anthu achuma ukunso mkusowa kwa chilungamo padziko lapansi. Izi zingatengere kuti chilungamocho chikufunidwa kuti. Mabwalo a milandu [MAKHOTHI] a dziko lapansi alephera kupereka chilungamo kwa anthu othodwa ndi wosowa chifukwa kuti satana ndi amithenga ake ndiwo akulamulira dziko lapansi.

Phunziro lathu la sabata yatha tinaona kuti Yesu akubwera kudzakhala mfumu yathu. Ndipo lero tionanso kuti Mulungu ndiye wachilungamo. Mulungu adzaweruzira dziko lapansi mosayang'ana nkhope, chuma, nzeru, maphunziro kudziwika kwa munthu, kuchuka, kapena mtundu ayi koma yense monga mwa ntchito zake. Chilungamo cha Mulungu chikuonetsedwanso pomwe akuchenjeza anthu onse za zochimwa zawo ndi chiweruzo chomwe chili mkubwera. Mulungu waikiratu mdima ndi kuunika kuti munthu asankhe choyenera kuchita chiweruzo chisanabwere.

## **MAFUNSO**

1. Kodi kwa inu achinyamata mukamva mau oti *chilungamo* amatanthauza chiyani? Kambiranani.
2. Fotokozani za kusoweka kwa chilungamo padziko lapansi nanga chiyembekezo chanu m'chotani pa nkhani ya kusoweka kwa chilungamo kumeneku?
2. Kodi ndi magulu ati awanthu womwe akusoweka chilungamo m'dera lanu lero nanga mungawalimbikitse bwanji?
3. Fotokozani ngati chilungamo chimapezeka kapena sichipezeka pa mpingo panu lero, chifukwa chiyani.?
4. Kodi Salmo-li likuimbidwa kwa ndani? Nanga mawu a mu vesu 2 akunenedwa kwa ndani?
5. Kambiranani momwe Mulungu akufotokozedwera m'mavesi amene tawerenga m'ndime yathu ya lero.
6. Tsimikizani kuti Mulungu ndi wachilungamo.

## **KUFOTOKOZA**

Kusoweka kwa chilungamo kwafika poipa m'nyengo zomwe tikukhalako ifezi. Anthu ambiri kuphatikizapo achinyamata akusowa mtendere chifukwa cha kusowa kwa chilungamo. Achinyamata ambiri sali pa ntchito ngakhale zowayenereza ali nazo chifukwa chakusowa kwachilungamo. Ana ndi amayi amasiye ali pa umphawi wadzaoneni chifukwa cha kusowa kwa chilungamo. Nthawi zambiri anthu wolembera ndiwo amapondereza anzawo chifukwa ndalama zawo ndizo zimalamulira. Anthu ena ngakhalsenso achinyamata amaganiza kuti anthu a ndale akhoza kubweretsa chilungamo koma izi zapezeka kuti sizoon.

Wolembera Salmo akutitsimikizira kuti Mulungu yekha ndiye ali wachilungamo ndipo adzaweruzira dziko lapansi mwa chilungamo. Yehova Mulungu wathu ali wopanda tsankho ndipo akufuna tonse tibwere kwa iye

ndi mtima wodzichepetsa. Pamene anthu tathodwa kulibenso kwina komwe tingapeze thandizo koma kwa Mulungu wathu yekha basi.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Dziko lapansi silipereke chilungamo ndi mtendere koma Mulungu wathu yekha, ndipo ife akhristu tikhale chitsanzo cha kuchita chilungamo nthawi zonse popembedza Mulungu wathu ndi kupereka zopereka zathu mwa chilungamo ngakhalenso kuthandiza osowa ndi a umphawi.

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Mateyu 24:1-25, 1 Petro 1 4:15-19, 2 Atesalonika 3:1-5, 1Yohane 1:1-9

**PHWANDO LOTSILIZA**

**Lemba la phunziro:** Chibvumbulutso 19:5-10

**Vesi Loloweza:** *Chibvumbulutso 19:6 Aleluya pakuti achita ufumu Ambuye Mulungu wathu wamphamvu yonse.*

**CHIYAMBI**

Shadreck, Mishek, ndi Abidinego anapulumutsidwa ndi Mulungu m'ng'anjo yamoto yotentha chifukwa chokana kulambira fano losema lopangidwa ndi mfumu Nebukadinezala mfumu yaku Babulo. Tayenera kukumbutsidwanso kuti kumapeto a nthawi ya pansi pano kudzakhalanso babulo wina. Babulo ameneyu adzachita chimodzi modzi poumiliza anthu kuti alambire fano la nthawi imeneyo, kulekana ndi kulambira mfumu yathu Khristu Yesu. Kudzakhala ulamuliro wamphamvu wakupha ndi wozunza anthu omwe akukana kulambira fanolo.

Munthawi imeneyi anthu ambiri adzaphedwadi ndi kuzunzidwa mosiyanasiyana. Koma pamapeto pake Mulungu adzaphwasula chilombo chimene chili Babulo ndi mkazi wa chigololo amene ali chipembedzo cha mafano. Anthu a pa dziko ndi angelo kumwamba adzalemekeza Mulungu kuchokera pamenepo onse amene anaphedwa ndi kunzuzidwa chifukwa cha fano losema adzayamba kuwakonzetsera phwando la Mwana wa Nkhosa. Mulungu adzatothoza onse mkati mwa phwandoli popeza sipadzakhalanso zowawa.

**MAFUNSO**

1. Kodi ndi ndani ananena mau amu vesi 5 ndipo akulankhula kwa ndani?
2. Kambiranani za mau omwe anamva Yohane ndipo fotokozani momwe mauwa adamvekera.

3. Fotokozani za ukwati wa mwana wa nkhusa zikutanthauza chiyani kwa inu achinyamata a lero?
4. Kodi mkwati ndi ndani ndipo mkazi wake ndi ndani?
5. Kambiranani za mgwirizano wa kukondwera ndi kesekera ukugwirizana bwanji ndi kulambira
6. Mukuganiza kuti anthu oitanidwa ku phwando lotsilizali adzakhala wotani?
7. Fotokozani za chimwemwe chanu ngati inu mutakhala m'modzi woyitanidwa kulowa mu phwando la mwana wa nkhusa.

## **KUFOTOKOZA**

Kubweranso kwa Yesu Khristu ndi chiweruzo Yohane 3:18, kwa osakhulupirira koma kwa okhulupirira ndi kukhala ndi Ambuye ku nthawi zonse, Aefeso 4:17. Mundime yathu ya lero tikuona mpingo monga ngati mkazi wa mwanawankhusa amene wadzikonzetsera yekha nayimira zolungama za oyera mtima. Chibvumbulutso 19:7-8. Odala ndi iwo amene ayitanidwa ku phwando la ukwati la [vesi 9] mwanawankhusa, awo ndiwo akukhala nawo umboni wa Yesu (vesi 10)

Achinyamata ambiri amafuna kukhala m'magulu momwe angathe kupeza zofuna ndi zosowa zawo kuti miyoyo yawo ithandizidwe. Koma ndi magulu ati amene tingapeze thandizo lenileni? Pofotokoza za phwando la ukwati wa mwanawankhusa ndi mkazi wake mu Chibvumbulutso 19, zikuonetsa kuti mpingo ndi malo ndi gulu loyenera m'mene tingathe kupeza thandizo lenileni la miyoyo yathu.

## **PHUNZIRO KWA IFE**

Achinyamata tayenera kukondwera mwa Mulungu pamene tikuyembekezera phwando lotsiliza pamodzi ndi Mulungu wathu.

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

1 Akorinto 5:1-10, 10:15-27, Yohane 7:8-37

**KUUNIKA KWA CHIKONDI**

**Lemba la phunziro** 1 Yohane 2:7-11, 15-17

**Vesi Loloweza:** *1 Yohane 2:10* Iye amene akonda m'bale wake akhala m'kuunika ndipo mwa iye mulibe chokhumudwitsa.

**CHIYAMBI**

Munthu wina anafunsa Yesu kuti lamulo loposa onse ndi liti, ndipo Yesu anayankha mwachindunji kuti lamulo loposa ndilo “udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako onse ndi mphamvu zako zonse ndi nzeru zako zonse ndipo lachiwiri lotsatana nalo udzikonda nzako monga momwe udzikondera iwe mwini”. Yohane sanatilembere ife lamulo latsopano ayi chifukwa lamulo la chikondi linalipo kuyambira pa chiyambi [1Yohane 2:7]. Yesu anatiphunzitsanso kuti tikondane nawo adani athu posabwezera choipa chilichonse. Lamulo lakuti diso kulipa ku diso tayenera kumusiyira Mulungu yemwe ali woweruza wolungama. Kukhala tiwana mmoyo wa uzimu ndiko kudana nalo tchimo ndipo kukhala wachinyamata m'moyo wa uzimu ndiko kum'gonjetsa satana posabwezera choipa koma ndi chabwino kugonjetsa choipa kumene kuli kuthawa tchimo. Khalidwe limeneli lisoweka kukhala wamphamvu ndi wolimbika mwa Yesu Khristu. Poto tikhala atate chifukwa kutero ndiko kudziwa Mulungu. Ichi m'chifukwa chake kuli kuunika kwa chikondi.

**MAFUNSO**

1. Fotokozani bwino lamulo lomwe Yohane akutilembera m'ndime yathu ya lero.
2. Kambiranani mau oti “*udani*”
3. Kodi mzotheka kumukonda munthu m'dani wako fotokozani?

4. Mukuganiza kuti mchifukwa chiyani Yohane akutiphunzitsa za lamulo la chikondi, nanga chikondi m'chofunika bwanji m'banja, pa m'pingo , kusukulu , m'mudzi kapena pa ntchito.
5. Kodi kukonda dziko lapansi kukutanthauza chiyani, kambiranani za anthu omwe inu mumaona kuti amakonda dziko lapansi
6. Nanga kukonda Mulungu kukutanthauza chiyani?
7. Kukambiranani za kusiyana kwa munthu amene amakonda Mulungu ndi munthu amene amakonda dziko lapansi

## **KUFOTOKOZA**

Kuwala kukhoza kuyimira chipulumutso komanso kuyenda m'moyo wa chiyero ndipo mdima ukhoza kuyimira kusadziwa komanso tchimo. Chofunika kudziwa m'chakuti kuwala nthawi zonse kumalumikizana ndi kupezeka kwa Mulungu ndi Khristu monga kuunika kwenikweni. Pamene munthu adana ndi m'nzake zimatsimikiza kuti munthuyo akuyenda mu mdima ngakhale kuti azionetsera ngati ali mkuwala. Baibulo limakamba za anthu awiri apachibale omwe ndi Kaini ndi Abale. Onse amkapereka nsembe kwa Mulungu pomwe Mulungu sanalandire nsembe ya Kaini koma ya m'bale wake Abele. Izi zikusonyeza kuti onse anali wopemphera koma Kaini anali kuyendabe mu mdima ndipo Mulungu sanalandire nsembe yake, Zotsatira zake Kaini anamupha m'bale wake Abele. Achinyamata ambiri tapha abale athu posawafunira zabwino, ngakhalenso kupha mpingo wathu posaufunira zabwino ndi kusapereka chuma chathu ku ntchito ya ambuye.

Ngati wina akonda dziko lapansi ameneyo alibe chikondi chochokera kwa Mulungu atate wathu. Pamene tikondana wina ndi m'nzake zimatsimikiza mmene chikhristu chathu chilili komanso kuyamika kwathu kwa Mulungu kuti Iye ndi amene anayamba kutikonda ife potipatsa mwana wake wobadwa yekha kuti adzatifere ndi kutiombola ku mdima wa uchimo wa dziko lapansi. Sitinganene kuti timakonda Mulungu pamene tikudana ndi anzathu



## **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu ndiye chikondi cheni cheni ndipo wompembedza iye ayenera kumupembeda m'chikondi

## **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

Machitidwe 26:1-20, 1 Akorinto 4:1-10, Aefeso 5:1-10, 1 Timoteo 6:1-16.

**KUITANIDWA KU CHIKONDI**

**Lemba la phunziro:** 1 Akorinto 13:1-13

**Vesi Loloweza:** *1 Akorinto 13:13 Ndipo tsopano zitsala chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitatu izi koma chachikulu cha izi ndi chikondi.*

**CHIYAMBI**

Chikondi ndi chiphunzitso chenicheni cha chikhristu. Yesu mwini anaphunzitsa za chikondi ndipo anatsindika kuti angakhale adani athu tayenera kuwakonda, ndipo popanda chikondi palibe chikhristu chifukwa chikondi ndiwo maziko a ufumu wa kumwamba. Pamene Paulo akuulembera mpingo waku Akorinto anafotokoza zambiri zomwe anthu odzitcha okha opembedza amachita mdzina loti ndi wopemphera ndipo Paulo sanatsutsane nazo koma akuwauza kuti koma ngati pakati pawo palibe chikondi ali chabe. Pakati pa achinyamata lero palinso tsankho lomwe lasefukira m’mpingo yambiri ndipo tsankho limabweretsa kudzikonda ndi kuwaona anthu ena ngati wosafunika ndi wopanda pake.

Chifukwa cha mphatso za uzimu zoperekedwa ku mpingo wa ku Akorinto mkati mwa akhristu munayamba maganizo akaduka, nsanje kunyozana ndi zina zambiri. Zoterezi zinafulumiza Paulo kulemba kalata yowadziwitsa kufunika kwa chikondi. Paulo anawauza kuti ngakhale adzitamandire ndi mphatso zomwe Mulungu anawapatsa koma alibe chikondi ali chabe chifukwa Mulungu ndiye chikondi. Pachifukwa ichi mu phunziro lathu la lero likutikumbutsa kuti ife achinyamata taitanidwa ndi kupatsidwa mphatso za uzimu kuti tigwiritse ntchito pokonda Mulungu ndi anzathu.

## MAFUNSO

1. Kambiranani zinthu zitatu zofunika pa moyo wathu wa chikristu, nanga mwa zinthu zitatu zimenezi chofunika kwambiri ndi chiti?
2. M'chifukwa chiyani ntchito za chikristu zili chabe ngati palibe chikondi?
3. Fotokozani kufunika kwa chikondi pa mpingo panu, m'mudzi mwanu pantchito panu, kusukulu kwanu.
4. Kambiranani momwe ife achinyamata tingagawanirane nawo anzathu chikondi chomwe Khristu Yesu adatipatsa ife .
5. Fotokozani kufanana kapena kusiyanana kwa *chikondi* ndi *kudzipereka* nsembe
6. Inu mungatsimikize bwanji kuti Yesu amakukondani, ndipo mungaonetse bwanji kuyamika kwanu kuti Yesu amakukondani.
7. Kambiranani momwe tingaonetsere chikondi kwa adani athu ife achinyamata, ndi kuonetsetsa kuti moyo wathu sulika pa chiopsezo.

## KUFOTOKOZA

Mulungu amafuna kuti ife achinyamata tidzikondana komanso osati kungokonda anasi athu okha koma ngakhale adani athu. Mateyu 5:43-45. Izi zikuonetsera kuti tayenera kukonda anthu ndi mtima wathu onse, ndi nzeru zathu zonse komanso ndi mphamvu zathu zonse. Chikondi cheni cheni sichikhala nazo zifukwa kwa wina ndi m'nzake. Nthawi zina pali anthu ena omwe sayamika ngakhale utawaonetsera chikondi chonse kwawo mkunyoza Paulo polemba Yesu akuti tidziwapempherera nthawi zonse. Yesu mwini adadziwa kuti palinso ena omwe ndi onyoza ndi opanda chikondi ndi anzawo ndipo akutilamulira kuti otere tidziwapempherera ndipo tisawatemberere. Yesu adaphunzitsanso kuti ngati mdani wako ali ndi njala um'dyetse ndipo ngati ali ndi ludzu umpatse madzi amwe. 1 Yohane 4:7-8

Ife achinyamata tayeneranso kukumbukira kuti pamene ife tinali chikhalire adani a Mulungu chifukwa cha uchimo Iye anatumiza mwana

wake kudzatifera ife kuthetsa udani pakati pa ife ndi Mulungu. Chotero ife tayitanidwa ku chikondi cha Mulungu ndipo ndi udindo wathu kuonetsera chikondi chimenechi kwa anzathu ngakhalenso akunja kuti nawo awone chikondi cha Yesu.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mulungu ndiye chikondi ndipo ngati ife tikhala mwa iye tayenera kuonetsa ndi chikondi chake

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUMBA**

1 Akorinto 7:1-20, Aefeso 1:1-18, Yeremiya 31:1-5, Miyambo 10:1-12

**CHIMWEMWE M'CHIKHULULUKIRO**

**Lemba la phunziro:** Masalmo 32:1-11

**Vesi Loloweza:** *Masalmo 32:1. Wodala munthuyo wokhulukidwa tchimo lake, wokwiridwa choipa chake.*

**CHIYAMBI**

Munthu ukakhala pa udani ndi munthu wina umasowa mtendere wa mumtima, iwe woda nzakowe ngakhalenso iye wodedwayo. Ngakhale timatha kudzilimbisa mtima ndi mau oti ndilibe naye ntchito, komabe mtendere sukhalapo. Kuti mtendere ubwerere pasoweka kukhululukirana. Kuti mtendere pasoweka kudzichepetsa ndi kupepesana ndipo apa ngakhale wolakwiridwa angathe kuyambitsa nkhani yokhululukirana.

Mulungu safuna kusungira munthu mangawa ndipo kukhululukira ndi mbali imodzi ya chikhalidwe cha Mulungu. Ngati achinyamata tiyendabe ndi mangawa ndi anzathu ndiye kuti kwa ife tikuyendabe mu mdima ngakhale kotale wathu akutilimbikitsa kuti tichoke mu mdima ndi kuyenda mkuwala. Achinyamata ambiri alibe nazo ntchito kuyenda mu mdima wa uchimo chifukwa chosafuna kuwakhululukira anzawo zoipa zawo nayiwala mwadala kuti Mulungu ndiye adayamba kutikhululukira ife zochimwa zathu natumiza Yesu Khristu kudzatiombola ife mu mdima wa uchimo ndi kutipatsa kuwala kwenikweni. Dziwaninso kuti mkwiyo wa munthu suchita chilungamo cha Mulungu.

**MAFUNSO**

1. Kodi wolembe Salmo atakhala chete ndi machimo ake anachita chiyani?
2. Kambiranani kuti mau oti “*Chimwemwe*” amanthauza chiyani?
3. Kambiranani zotsatira za kuvomereza kwake kuti zinali zotani?

4. Fokokozani zizindikiro zingapo zosonyeza kuti munthu wakhululukidwa machimo ake ndi kuti zoipa zake zakwiriridwa.
5. Fotokozani za langizo lomwe laperekedwa mu vesi 8-11.
6. Ife monga achinyamata langizoli lingatithandize bwanji m'moyo wathu wa lero?

## **KUFOTOKOZA**

Salmo ili linalembedwa ndi Davide yemwe anali munthu womvetsa kuti kukhululukidwa ndi chiyani. Cholinga chake ndicho kuti apeze chimwemwe pomwe cholakwa chake chakhululukidwa. Ndipo kunali kosavuta kuona kuti anali wodzazidwa ndi chimwemwe. Nthawi imene Davide anazindira tchimo lake kulakwa kwake kunachoka. Kuvomereza tchimo kwa Mulungu ndi mtima onse kumabweretsa chikhululukiro. Ichi ndi chimodzi mwa mphatso zopatsidwa kwa munthu. Nthawi zina timayika kulakwa kwathu pamapazi a anthu ena, kapenanso kunyalanyaza osavomereza, koma tidziwe kuti pamene munthu wavomereza tchimo lake amalandira chikhululukiro. Achinyamata tiyeni tikhale ngati Davide ndi kuvomereza zochimwa zathu pamene tikuchoka mu mdima ndi kulowa m'kuwala kodabwitsa kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Chimakhala chimwemwe choposa kumwamba munthu m'modzi akatembenuka mtima ndi kubwera kwa atate. Zindikiraninso kuti malemba amatitsimiikizira kuti tikati kuti tilibe uchimo tidzinyenga tokha ndipo mwa ife mulibe choonadi. Achinyamata tikukhala m'masiku ovuta omwe zochikika za dziko lapansi ndi zambiri ndipo izi mzofuna kutitayitsa Yesu wathu, choncho tiyeni tikhale maso kuona momwe dziko likupitira ndi kukhala wochenjera monga ngati njoka ndi wowona mtima monga ngati nkunda.

## **PHUNZIRO KWA IFE**

Kuchimwa kumakhudza munthu wina aliyense chimodzimodznsso kukhululukidwa kumakhudzanso munthu wina aliyense. Tikavomereza machimo athu onse Ambuye adztikhululukira zochimwa zathu ndipo

tidzakhala ndi chimwemwe. Tiphunzirensa kukhululukira anzathu omwe atilakwira monga momwe Mulungu apangira ndi ife.

## **MALEMBA WOWERENGA KU NYUMBA**

Yakobo 5:1-11, Yobu 5:1-17, Masalmo 127 :1-5, Deuteronomo 33:25-29

**KUKHULULUKIRANA**

**Lemba la phunziro:** 2 Akorinto 2:5-11, 7:2-15

**Vesi Loloweza:** *2 Akorinto 7:10 Pakuti chisoni cha kwa Mulungu chitembenezira mtima ku chipulumutso, koma chisoni cha dziko lapansi chichita imfa.*

**CHIYAMBI**

Kotale wathu tatsindika za kuchoka mu m'dima ndi kulowa mu kuunika kodabwitsa kwa Ambuye wathu Yesu Khristu komanso kuti Mulungu amakhala pakati pa anthu ake. Taonamonso za kwathu kwatsopano ndi phwando lotsiliza zomwe zikuonetsa kuti tili ndi mudzi wina womwe ife tikuyembekeza kudzalowamo ndipo kulibe mdima. Koipa kena kalikonse sikadzalowako ndipo tidzakhala anthu wokondwa nthawi zonse.

Pachifukwa ichi tayenera kudandaulirana wina ndi m'nzake za moyo womwe tikukhalawu kuti wina asapite ku dzanja la manja kapena lamanzere koma tonse tiyende ulendo wabwino kukakomana naye mbuye wathu. Posinkha-sinkha za moyo uno takhumudwitsana wina ndi m'nzake ndipo tikuyenera kukhululukirana kuti tidzapezeke wopanda banga ndi chilema pamaso pa Mulungu wathu

Pamene Paulo analamulira kuti munthu wa chigololo achotsedwe mu mpingo wa ku Akorinto, anthu ena mu mpingowo sanakondwere nazo kotero kuti mapokoso anakula ku mipingo yonse ya ku Akorinto. Ndipo Paulo analemba kalata imene inathetsa mapokoso onse ndi kukhala mpingo yosinthika ndi moyo wa uzimu. Ndipo Paulo akuyamikira kusinthika kwa mpingowo kuti unali ndi fungo labwino. Ndi udindo wathu kukonza zolakwika mu mpingo ndipo pokonza pamakhala kukhumudwitsana koma zonse zikatha tiyenera kukhululukirana ndi kuyambanso mwatsopano.



## **MAFUNSO**

1. Fotokozani za mitundu iwiri ya chisoni yomwe Paulo waitchula m'ndime yathu ya lero.
2. Kambiranani kusiyana kwa mitundu iwiri ya chisoni yomwe yatchulidwa mu ndime yathu ya lero komanso za kufunika kwake.
3. Kambiranani ngati kunali kofunika kuti Paulo achite kuulembera mpingo wa ku Akorinto za kukhululukirana, ndipo perekani chifukwa cha yankho lanu.
4. Fotokozani njira zomwe mungatsate pobwezeretsa ubale omwe udasweka pakati panu monga achinyamata
5. Inu mukuganiza kuti ndi ndani angalandire chikhululukiro cha zolakwa zake.
6. Kodi mungathe kumukhululukira bwanji munthu amene sanapemphe chikhululukiro kwa inu?
7. Kambiranani kufunika kokhululukirana ndi kuchotserana mangawa onse pakati pathu monga akhristu

## **KUFOTOKOZA**

Paulo akutiiza kuti pamene tikhululukirana wina ndi m'nzake tiyeneranso kuonetsa chikondi kwa wina ndi m'nzake komanso kutonthozana. Chinthu chinanso chofunika pa chikhululukiro ndicho kuvomereza. Paulo ananyadira kuona kuti Akorinto anavomereza kulakwa kwawo ndipo anapempha chikhululukiro. Kusakhululuka kumaphwanya ubale wathu ndi Mulungu. Nthawi zambiri achinyamata timakana kuvomereza kuti talakwa kapenanso kuti zinthu sizikutiyendera bwino m'malo mopempha Mulungu kuti atikhululukire timaona ngati njira yabwino koma kudzimangirira. Ukunso kumakhala kupalamula mulandu wina pamaso pa Mulungu popeza Mulungu sakondwera nayo mitima yosalapa.

Mkwiyo wa munthu suchita chilungamo cha Mulungu ndipo pomwe tikhala wosawakhululukira anzathu timaononga ubale wathu ndi Mulungu. Nthawi zonse tidzikumbukira kuti ndife wolephera ndipo tisanayambe

kudana ndi anzathu womwe akutidzudzula tiyambe tasinkha-sinkha pa zomwe tachita ndipo tisadziweruze kuti ife sitinalakwa koma tivomerezane wina ndi nzake kuti machimo athu akhululukidwe pamaso pa Mulungu.

### **PHUNZIRO KWA IFE**

Mkwiyo umaononga ubale wathu ndi Mulungu ndipo tayenera kuchotsa mkwiyo pokhululukirana ndi anzathu kuti ubale wathu ndi Mulungu ukhale wabwino

### **MALEMBA WOWERENGA KUNYUNMBA**

Mateyu 6: 9-15, Mateyu 18: 21-35, Aefeso 3:12-17, 2 Akorinto 2:5-11, 2 Akorinto 7:8-16



